

KUSANKHA KWA MKWATIBWI



Anthu odwala ambiri. Sindingakhoze kufika kwa onse awo mwakamodzi. Koma, mvetserani.

² Ndine ndithudi wokondwa kuti ndiri pano kachiwiri, usikuuno, mu nyumba yoyankhuliramo yokongola iyi, pakati pa gulu lodabwitsa ili la anthu. Ndipo ife tinali kulowa muno, kunja uko, mphindi pang'ono zapitazo, anthu ataimirira uko ku msewu iwo amati samakhoza kulowa muno. Ndipo ine ndinati, “Chabwino, mwinamwake ine ndikhoza kukupezerani inu malo ena.” Ndipo sanawalole iwo kuti abwere kuno. Kotero ndine wo pepesa kuti ife tiribe malo okwanira kwa iwo. Iwo anati malo apansi anali odzaza, nawonso. Ndipo kotero ndife opepesa pa izo. Koma ndife okondwa kukhala tiri pano, ndi okondwa kuliwona gulu lonse labwino ili la atumiki, amuna amalonda kuno, ndi inu nonse nthumwi zochokera ku mbali zosiyana za dziko.

³ Ine ndinali nawo mwayi waukulu wa kuyankhula mmawa uno pa kadzutsa, chomwe ine ndithudi ndikuchiyamikira kuti ndi cha ulemu kuyankhula pamaso pa anthu abwino choterowo. Ine ndinali pa phunziro la: *Mankhusu Sadzalowa Ufumu Palimodzi ndi Tirigu*. Ine sindinafike politsiriza ilo. Ndipo ilo silinali v—vuto la m'baleyo. Iye anayesera kuti awapeze olamulira kuti atiloleze ife tikhale motalikirapo pang'ono, koma iye basi sakanakhoza kuchita izo. Ine ndithudi ndikuyamikira izo, M'bale Demos. Ndizo kwambiri, zabwino kwambiri. Ine ndithudi ndikukuthokozani inu chifukwa cha chifundo chanu, mmodzi ndi aliyense. Koma iwo basi sakanatilola ife kuti tichite izo. Kotero ife basi tina—tinangotseka. Ine ndidzazitenganso izo, nthawi inayake, kuti ndidzatsirizitse izo: *Mankhusu Sadzalowa Ufumu Palimodzi Ndi Tirigu*. Kodi inu munazimvetsa izo, inu omwe munali kuno? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Ine ndikuyembekeza zinalipo zokwanira zomwe zikanati zimvetsedwe.

⁴ Tsopano, ine ndikudziwa, usikuuno, pali gulu lokambirana, naponso, kotero ine sindikufuna kuti ndikusungeni inu pano utali wokwanira kuti inu muziphonye izo. Chifukwa, ine ndikuganiza kuti izo zinali ndithudi c—chofunikira k—kwa anthu okhulupirira Achipentekoste, gulu lokambirana lija lomwe ife tinaliwona usiku wina uja. Gulu labwino loterolo la amuna, mayankho odabwitsa otero aja, olunjika. Izo zinandipangitsa ine kumverera mwabwino kwenikweni, poziwona izo. Ine ndikudalira kuti Ambuye azidalitsa izo, usikuuno. Ndipo yense yemwe ati apenye izo, iwo atati akhulupirire. Ilo lingakhale pemphero langa lodzipereka.

⁵ Ndipo maripoti ochuluka kwambiri akubwerapo, lero, ochokera mu makalata ndi kuitana, kwa ochuluka kwambiri pokhala atachiritsidwa mu msonkhano uno. Ine ndinali wokondwa kwambiri ndi izo. Izo, ndizo, kuwawona anthu odwala, ndiwo mtundu wa utumiki wanga.

⁶ I—ine ndimabwera kuno kuti ndidzalalikire. Ine, inu mukudziwa, ine sindine mlaliki. Koma ine, ndi iyi, galamala yanga yaku Kentucky, “his, hain’t” n—ndi mawu onse awo, chotero i—ine sindingakhoze kunena monga zomwe ife timazitcha mlaliki wamakono wa lero. I—ine sindingakhoze kutenga malo amenewo, chifukwa i—ine ndiribe maphunziro.

⁷ Koma ine ndimakonda kufotokoza zomwe ine ndikudziwa za Iwo, kwa ena, kapena zomwe ine ndikumverera kuti ine ndikuzidziwa za Iwo, kwa ena, momwe ine ndawaphunzirira Iwo, momwe Iye aliri kwa ine. Iye ali moyo wanga wonse, zonse zomwe ine ndikanaziyembekeza konse kuti zikhale ziri, ndi zochuluka kwambiri kuposa zomwe ine ndinaziganizirapo konse, kuti ine ndikanadzakhala naye mzanga konse, nkomwe, pa dziko lapansi, pamene ine ndinali mnyamata wamng’ono. Koma ine ndithudi ndine wothokoza chifukwa cha abwenzi opambana lero.

⁸ [M’bale akuti, “Tiri ndi vuto pang’ono la kumva kumbuyo uko, M’bale Branham. Muyandikiremo pafupi.”—Mkonzi.] O, ine ndikupepesa. I—ine ndikukhala ngati ndikuloza kumbali, kwinakwake, iye amatero.

⁹ Tsopano, kuti tifike kumene molunjika mu utumikiwu, tiyeni titembuzire ku kuwerenga kwa Lemba kwina. I—ine nthawizonse ndimakonda kuliwerenga Baibulo, chifukwa Ilo ndi Mawu a Mulungu. Ine ndikukhulupirira zimenezo. Ndipo ine ndikukhulupirira kuti Ilo liri Mawu osalephera a Mulungu. Ndipo tsopano ine ndiri nao Malemba angapo ndawalemba apa pano, ndi zolemba zina zomwe ine ndikufuna kuti ndizionerapo, kwa mphindi zingapo, mwinamwake kwa maminiti forte-faifi.

¹⁰ Ndiyeno ife tituluka mu nthawi yabwino kuti tikaliwone gulu lokambirana lodabwitsa ili kachiwiri usikuuno. Ndipo ine ndikudalira kuti Mulungu apitiriza kukudalitsani inu pomwepo podutsa nazo. Ndipo ine ndikudziwa chimene inu mukuyenera kuti muchichite. Ndipo ine ndikuyenera kuti ndiyendetse kupita ku Tucson, panobe, usikuuno, onani, kotero inu mukhoza kulingalira. Uko ndi kuyendetsa kwa maora teni.

¹¹ Ndipo ine ndikuchoka kupita ku tsidya kwa nyanja, ndipo ine ndiyenera kuti ndikalandire katemera wa chintchofu pa kupimidwa mmawa ku boma. Kotero i—ine ndiyenera kuti ndikafike kumeneko. Ine ndinachita kusintha tsiku, tsiku lina, ndipo iwo sakatenga “ayi” ngati yankho kachiwiri tsopano. Ndipo ine ndatsala ndi ya nthomba ndi zipere kuti ndikaitenge, ndi zondilimbikitsa zanga.

12 Kotero, ine ndiri wothokoza kwambiri chifukwa cha mwayi uwu, n—ndi msonkhano wabwino uwu umene ife tinali nawo usanachitike msonkhano waukulu. Izo ndithudi zinakondoweza mtima wanga. Ndinu gulu labwino la anthu. Ine ndikudalira kuti Mulungu akudalitsani inu.

13 Pamene ora lalikulu liti . . . Chinapolo chachikulu chija chiri kutsidya uko, chimene chinadzipiringizira chokha ku Alaska, masiku angapo apitawo, chinaponyera mchira wake mmwamba kachiwiri mmawa uno, motsatira choncho, kufika cha ku Washington. Iye akhoza kulunjika wa kuno, ndi mphamvu mophweka. Ndipo ngati Mzimu Woyera uti undiuze ine konse motsimikiza . . .

14 Winawake wakhala akuyankha . . . akundifunsa ine izo, “Kodi izo zidzachitika kuno, M’bale Branham?” Ayi, ine sindikudziwa izo. Ine sindikudziwa basi, mpaka ine nditadziwa. Icho ndi choonadi.

15 Ine nthawizonse ndafuna kuti ndizikhala woonamtima ndi inu. Ine sinditi ndizipita mopenekera basi, kutenga lingaliro lirilonse, kapena zina, chimene ine ndikuchikhulupirira, kapena chinachake chonga izo. Pamene ine ndikuuzani inu, izo zidzakhala ziri. Chabwino, Iye amayenera kuti andiuze ine, poyamba, ndiyeno ine ndingakuuzeni inu. I—ine ndikudziwa dziko lonse liri mu chikhalidwe chogwedezeka. Ife tiri pa nthawi ya kumapeto. Koma chinthu chimodzi chomwe ine ndayesera kuti ndikhale . . .

16 M’bale Shakarian anali kunena mmawa uno, momwe iye ankadutsira mu mizere ya pemphero, ndi kufikira apo ndi kukawatenga makadi awo anthu asanabwere apo, ndi kuyang’ana pa iwo, ndi kuwona ngati—ngati ine ndinawawuza iwo zomwe iwo anali atazilemba pamenepo. Iwo amalemba mitundu yonse ya zinthu pa makadi awo a pemphero, inu mukudziwa, ndipo iye ankafuna basi kuti aziwona ngati izo zinali zolondola. Iye anati, kuchokera mwa mazana omwe iye anali atawafufuza, sipanakhale pali chimodzi cholakwika. [M’bale Shakarian akuti, “Panalibe chimodzi cholakwika.”—Mkonzi.] Sipadzakhala konse chimodzi cholakwika, onani, chifukwa, b—bola ngati ali Mulungu. Ngati ine ndikanakhala ndikudzionetsa konse ndekha mu izo, ndiye ndi zolakwika apo pomwe pa kuyamba pomwe.

17 Msungwana wamng’ono yemwe bambo ake akhala, akumvetsera kwa ine pano, anabwera kwa ine, osati kale litali. Iye anali ndi loto. Iye anati, “M’bale Branham, kodi loto ili likutanthauza chiani?”

18 Ine ndinati, “Ine sindikudziwa, mlongo. Ine ndiyenera kuti ndikafufuze, ngati Ambuye ati andiuze ine.” Kotero ine ndinapitirira ndi kuyesera kuwafunsa Ambuye, ndipo Iye sanandiuze konse ine.

¹⁹ Msungwana wamng'onoyo anabwereranso kachiwiri. Iye anati, “Chabwino, tsopano kuli kuti kutanthauzira kwa loto langa?”

²⁰ Ine ndinati, “Bwera kuno, wokonedwa, khala pansi.” Ine ndinati, “Bambo ako ndi amako ndi abwenzi abwino kwambiri a ine. Waona? Ndipo iwo anabwera njira yonse kuchokera ku Canada, atapuma pa ntchito, ndipo anadzayenda kuno ndi ine. Iwo amakhulupirira izi, zomwe ine ndikuyesera kuzinenazi. Ndipo ine sindinayambe ndanenapo chirichonse cholakwika kwa wina aliyense, mwadala, mu moyo wanga. Ngati ine...ine ndikuganiza ine ndikudziwa chimene lotolo likutanthauza. Koma mpaka ine nditaliwona loto limenelo mwiniwanga, ndiyeno Iye amaandiuza ine chimene ilo likutanthauza, ine sindingakhoze kukuza iwe. Mwaona, ngati ine ndingopeka chinachake, pakhoza kudzakhalala nthawi yomwe iwe ungasandifune ine pakati pa moyo ndi imfa, ndiyeno iwe sukanadzadziwa kaya kuti undikhulupirire ine kapena ayi.”

²¹ Ngati ine ndikuuza iwe chirichonse mu Dzina la Ambuye, izo ndi zoonadi momwemo. Uyo ndi Yemwe anandiuza ine izo. Ndipo mpaka pano, mu zaka zonse izi, kudutsa mu dziko lonse, ndi kuzungulira dziko, Izi sizinayambe zakhala zolakwika nthawi imodzi. Izo zimadula...Ndipo, tsopano, inu mukudziwa munthu wokhalapo sangakhoze kukhala wosalephera chotero. Izo zimatengera Mzimu wa Mulungu kuti uchite izo.

²² Ndipo tsopano ine ndiri ndi Uthenga umene ine ndiri nawo choyankhira. Ndipo nthawi zambiri ine ndakhala ndikutengedwa, pakati pa anthu, chabwino, mwinamwake winawake yemwe sanakhale pansi ndi kulingalira kwa miniti, kuti ine ndinali—a, o, munthu woipa, ine sindimawakonda anthu, ndipo ine nthawizonse ndinali kuwacheka iwo. Ndipo izo siziri chomwecho. Izo siziri chomwecho. Ine ndimawakonda anthu. Koma, inu mukudziwa, chikondi ndi chokonza.

²³ Ngati mnyamata wanu akanati akhale pa msewu kunjja uko, ndipo inu nkuti, “Junior, wokonedwa, ine sindikufuna iwe kukhala kunjja uko, koma...” Ndipo magalimoto akulindima pafupi naye, ndipo inu mutamubweretsa iye mkati. Iye nathamangiranso kunjja uko kachiwiri. Bwanji, inu muyenera kumukonza iye. Ngati inu mumamukonda iye, inu mutero. Inu muyenera kutero.

²⁴ Ngati inu mutamuwona munthu akuyandama chotsika mu mtsinje, akupita ku mathithi, mu ngalawa yaing'ono, yomwe inu mukudziwa kuti ngalawa iyo ikukamira pamene iyo ikafika ku mathithi, kodi inu mukanati, “John, iwe, mwinamwake ukuyenera kuti uganize kanthawi, mwinamwake iwe sukakwanitsa apo?” Ngati ine ndikudziwa kuti iye sakakwanitsa apo, ine ndingakhale pafupi kumugwedeza iye

kuti achoke mu ngalawayo, ngati ine ndingakhoze, chifukwa ndi chikondi chimene chimachititsa izo.

²⁵ Ndipo tsopano, mu Mauthenga awa amene ine ndikuwayankhula, ine sindimayesera nkomwe kuti ndibweretsemo chiphunzitso chirichonse, kapena zina zotero. I—ine ndimachita izo mu mpingo wanga womwe. Koma kunja kuno pakati pa amuna ndi akazi omwe ali azipembedzo zosiyana ndi malingaliro osiyana, ine ndimangoyesera kuti nditenge zamawonekedwe apakati, kuti ndifotokoze; koma mokwanira mpaka pamene ngati iwe uli wobadwa ndi Mzimu wa Mulungu, ine ndikukhulupirira iwe ungamvetse zomwe ine ndikutanthauza, pakati pa amuna Achikristu, Amethodisti, Abaptisti, Achipresbateria, ena onse.

²⁶ Tsopano, usikuuno, ine ndikufuna kuti nditembenuzire ku Genesis, mutu wa 24. Ine ndikufuna kuti ndiwerenge... kuyambira ndi ndime ya 12 ya mutu wa 24 wa Genesis.

Ndipo iye anati, O YEHOVA Mulungu...mbuye wanga Abrahamu, ine ndikukupemphani inu, mundipatse ine livilo labwino lero lino, ndipo muwonetsere chifundo kwa mbuye wanga Abrahamu.

Taonani, ine ndiima pano pa chitsime cha madzi; ndipo ana aakazi a anthu a mmudziwu abwera kuno kudzatunga madzi:

Ndipo mulole kuti zifike pochitika, kuti namwali kwa yemwe ine ndidzati, Tsitsa pansi mtsukowo, ine ndikukupempha iwe, kuti ine ndikhoze kumwa; ndipo iye akati, Imwa, ndipo ine ndizipatsa ngamila zako zimwe nazonso: mulole; yemweyo akhale iye amene inu mwamusankhira wantchito wanu Isake; ndipo pamenepo ine ndidzadziwa kuti inu mwandionetsa ine chifundo kwa...cha kwa mbuye wanga.

²⁷ Ndiyeno mu Bukhu la Chivumbulutso. Lijali ndi loyambirira la Baibulo, Genesis. Tsopano, kotsirizira kwa Baibulo, ine ndikufuna kuti ndiwerenge mu mutu wa 21 wa Chivumbulutso, ndi ndime ya 9.

²⁸ Ife tikudziwa chomwe Lemba ili la Genesis pano...Inu muwerenge mutu wonsewo, ngati inu mukufuna kutero. Ndi Mulungu atamutuma Eliezere. Kapena, Abrahamu atamutuma Eliezere, ndikhubelukireni ine, kuti akasankhe mkwatibwi wa Isaki. Ndipo Rebeka wokongola anatulukira uko, ndipo anali mwangwiro yankho la kwa pemphero lija—lomwe Eliezere, wantchito wa Abrahamu, anali atangolipemphera.

Tsopano mu ndime ya 9 ya mutu wa 21 wa Chivumbulutso.

Ndipo apo anadza kwa ine mmodzi wa angelo asanu ndi awiri omwe anali ndi mbale zisanu ndi ziwiri zodzaza ndi maliri isanu ndi iwiri yotsiriza,

ndipo anayankhula ndi ine, nati, Bwera kunoko, ndipo ine ndikusonyeza iwe mkwatibwi, mkazake wa Mwanawankhosa.

²⁹ Tsopano ine ndikufuna kuti nditenge mwa phunziro, usikuuno, kwa izo: *Kusankha Kwa Mkwatibwi*. Ndipo uwu ndi, ngati m'bale wanga yemwe akujambula pano akufuna, iyi ndi tepi yomwe inu mukhoza kupitirira nayo ndi kuitulutsa iyo.

³⁰ Tsopano, mu izi, izo sizikutanthauza ndendende kuti ine ndikuyankhula izi kwa gulu ili lomwe liripoli, koma matepi awa amapita kuzungulira dziko. Iwo amamasuliridwa, mochtika, o, gawo lalikulu la zinenero, ngakhale mu maiko achikunja kuzungulira dziko. Ife timawatumiza matepi amenewo, mwaulere, ku gulu la mpingo. Ndipo iwo amakamasuliridwa. Ndipo konse kunja kudutsa mu nkhalango za Afrika, ndi mpaka ku India, ndi kuzungulira dziko, amapitako matepi amenewa.

Tsopano, kusankha Mkwatibwi!

³¹ Mu zinthu zambiri za moyo ife timapatsidwa kusankha. Njira ya moyo, payokha, ndi kusankha. Ife tiri ndi ufulu wopanga njira yathu yathu, kusankha njira yathu yathu yomwe ife tikuifuna kuti tizikhallira moyo.

³² Maphunziro ndi kusankha. Ife tikhoza kusankha ngati tikufuna kukhala ophunzira, kapena ngati ife sitikhala tiri ophunzira. Uko ndi kusankha komwe ife tiri nako.

³³ Chokhoza ndi cholakwika ndi kusankha. Mwamuna aliyense, mkazi aliyense, mnyamata ndi msungwana, ayenera kuti asankhe ngati iwo ati ayesere kumakhala molondola kapena kusamakhalala molondola. Ndi kusankha.

Kusankha ndi chinthu chachikulu.

³⁴ Kopita kwanu Kwamuyaya ndi kusankha. Ndipo mwinauwake, usikuuno, ena a inu mukupanga uko—kusankha uko, kwa komwe inu muti mudzakakhale Mwamuyaya, utumiki uwu usanatthe usikuuno. Padzakhala nthawi imodzi, yoti, ngati inu mumukana Mulungu nthawi zambiri, padzakhala nthawi imodzi yomwe inu muti mudzamukane Iye kwa nthawi yotsiriza. Pali mzere pakati pa chifundo ndi chiweruzo. Ndipo ndi chinthu chowopsya kwa mwamuna kapena mkazi, mnyamata kapena msungwana, kuti aponde kudutsa mzere umenewo, pakuti palibe kubwerera pamene inu muponda kudutsa mzere wa imfa uwo. Koteru, usikuuno, iyo ikhoza kukhala ili nthawi yomwe ambiri ati apange kwawo—kusankha kwawo, kumene iwo ati adzakakhale Mwamuyaya wosatha.

³⁵ Pali kusankha kwina kumene ife tiri nako mu moyo, ndiye, mzako wamoyo. Mnyamata kapena msungwana, yemwe akufika mu moyo, wa—wapatsidwa ufulu wopanga kusankha. Mnyamata amasankha. Msungwana ali nawo ufulu kuti avomereze kapena

kukana izo. Koma uko ndi kusankhabe, ku mbali zonsezo. Onse mwamuna ndi mkazi, iwo ali nao ufulu wa kusankha.

Ndiponso, inu muli ndi kusankha, monga Mkhristu.

³⁶ Inu muli nako kusankha kwa mpingo, muno mu Amereka, mpaka pano, kumene inu mungati muzipitako. Uwo ndi mwayi wanu wanu wa Chimereka, kuti muzisankha mpingo uliwonse umene inu mukufuna kuti mukhale wa iwo. Uko ndi kusankha. Inu simumasowa kuti muzipita ku wina uliwonse wa iyo, ngati inu simukufuna kutero. Koma ngati inu mukufuna kusintha kuchokera ku Methodisti kupita ku Baptisti, kapena Katolika kupita ku Chiprotestanti, kapena zina zotero, palibe winawake yemwe angakhoze kukuuzani inu kapena kukupangitsani inu kumabwera ku mpingo wina uliwonse. Uwo ndi wathu—uwo ndi ufulu wathu. Ndi chimene demokarase yathu ili. Munthu aliyense akhoza kudzisankhira yekha. Ufulu wa chipembedzo, ndipo ndicho—chinthu chachikulu. Mulungu atithandize ife kuti tizisunge izo utali wonse womwe ife tingakhoze.

³⁷ Inu muli nakonso kusankha. Kaya . . . Pamene, inu musankha mpingo uno, inu mukhoza kusankha kaya inu, mu mpingo uno, kaya inu musankha mpingo womwe uti ukutsogolereni inu mpaka kopita kwanu Kwamuyaya. Inu mukhoza kusankha mpingo umene uli ndi kachikhulupiriro kena kake, komwe inu mukhoza kuganiza kuti kachikhulupiriro ako kali basi chimene inu mumafuna. Kapena, mpingo wina uli ndi kachikhulupiriro kawo.

³⁸ Ndiyeno pali Mawu a Mulungu, omwe inu muli nawo kusankha kwake. Inu mumayenera kupanga kusankhako.

Pali lamulo losalembedwa pakati pathu, la kusankha.

³⁹ Ine ndikukhulupirira anali Eliya, nthawi ina, pamwamba pa Phiri la Karimeli, chitachitika chiwonetsero, mu ora lalikulu la zovuta lomwe ife tiri pafupi kuti tibweremo pakali pano. Mwinamwake, iyo ikhoza kukhala kwa inu kapena ine, usikuuno, kuti tipange kusankha uku, monga chochitika cha pa Phiri la Karimeli. Moona, ine ndikuganiza izo zikuchitika, mu dziko kulikonse, tsopano. Koma posachedwapa pakhala nthawi yomwe inu musowa kuti mupange kusankha.

⁴⁰ Ndipo inu amuna pano, a mipingo yanu ya zipembedzo, ingokhulupirirani izi, kuti ora liri pa inu pomwe, pamene inu muti mupange kusankha. Inu mwina mudzapita mu Khonsolo ya m'Dziko, kapena inu simudzakhala konse chipembedzo aponso. Inu mudzayenera kudzapanga izo, ndipo kusankha kumeneko kukubwera posachedwa.

⁴¹ Ndipo ndi chinthu chowopsya kuti udikire mpaka ora lotsiriza ilo, aponso, chifukwa inu mukhoza kutengera chinachake chimene inu simungakhoze kudzisansa kwa icho. Inu mukudziwa, pali nthawi yomwe inu mungakhoze kuchenjezedwa, ndiye, ngati inu muwoloka kudutsa mzere uwo

wa kuchenjeza, ndiye inu mwaikidwa kale chizindikiro cha ku mbali inayo, kupsyepsyerezedwa.

⁴² Kumbukirani, pamene chaka cha chisangalalo chibwera, ndipo w—wansembe anakwera ndi kuwomba kwa lipenga lake, kuti kapolo aliyense akanakhoza kupita ali mfulu. Koma ngati iwo akana kuti avomereze ufulu wawo, ndiye iye ankayenera kuti atengedwere ku kachisi, ku nsanamira, ndipo chisongole chimamubowola iye mu khutu, ndiyeno iye ankatumikira mbuye wake nthawizonse. Icho chinkaikidwa pa khutu lake ngati choimira, cha kumva. “Chikhulupiriro chimadza pa kumva.” Iye analimva lipenga lija, koma iye sanali kufuna kuti amvetsere kwa ilo.

⁴³ Ndipo nthawi zambiri, amuna ndi akazi amamva Choonadi cha Mulungu, ndipo amachiwona Icho chikuvomerezedwa ndi kutsimikizidwira, Choonadi, komabe iwo samafuna kuti amvere Icho. Pali chifukwa chinachake. Pali kusankha kwina kwake kumene iwo ali nako, kuposa kuti ayang’anizane nacho Choonadi ndi zoonza, chotero makutu awo akhoza kutsekedwera kwa Uthenga. Iwo sadzawumvera konse Iwo kachiwiri. Langizo langa kwa inu, pamene Mulungu ayankhula kwa mtima wanu, inu muzichitapo apo pomwe.

⁴⁴ Eliya anawapatsa iwo kusankha komwe iwo akanayenera. “Sankhani inu lero yemwe muti muzimutumikira. Ngati Mulungu ali Mulungu, zimutumikirani Iye. Koma ngati Baala ali Mulungu zimutumikirani iye.”

⁴⁵ Tsopano, pamene ife tikuwona kuti zinthu zonse zachibadwa ndi zoimira za zinthu zauzimu, monga ife tinadutsira mu phunziro lathu mmawa uja, monga dzuwa ndi chikhalidwe chake. Limenelo linali Baibulo langa loyamba. Ine ndisanawerenge konse tsamba mu Baibulo, ine ndinkamudziwa Mulungu. Chifukwa, Baibulo linalembedwa paliponse mu chilengedwe, ndipo izo zimangogwirizana ndi Mawu a Mulungu: momwe imfa, kuikidwa mmanda, chiwukitsiro cha chirengedwe, ndi dzuwa kutuluka, kudutsa, kukalowa, kufa, kutuluka kachiwiri. Pali zinthu zochuluka kwambiri zomwe ife tingakhoze kuzifanizitsira, Mulungu mu chilengedwe, zomwe ife tiyenera kuzilambalala, chifukwa cha Uthenga uwu.

⁴⁶ Tsopano, ngati zauzimu kapena...Zathupi ziri zoimira zauzimu. Ndiye, kusankha kwa mkwatibwi, mwa chibadwa, ndi choimira cha kusankha Mkwatibwi, Mkwatibwi, mwa uzimu.

⁴⁷ Tsopano, ndi chinthu chotsimikiza pamene ife tipita kukasankha mkazi, mwamuna, pakuti malumbiriro apa ali mpaka imfa mpomwe ife timalekana. Ndi momwe ife tiyenera kumalisungira ilo. Ndipo inu mumatenga lumbiriro limenelo pamaso pa Mulungu, kuti imfa yokha ndiyo idzakulekanitsani inu. Ndipo ine ndikuganiza ife tiyenera. Mwamuna mu kuganiza kwake kolondola, yemwe akukonzekera tsogolo, kuti iye ayenera

azimusankha mkazi ameneyo mosamala kwambiri. Muzisamala zomwe inu mukuchita. Ndipo mkazi akamasankha mwamuna, kapena kuvomereza kusankha kwa mwamuna, ayenera kukhala wosamala kwenikweni pa zomwe iye akuchita, ndipo makamaka mu masiku ano. Mwamuna ayenera kuganiza ndi kupemphera iye asanamusankhe mkazake.

⁴⁸ Ine ndikuganiza, lero, zomwe zatengera milandu yochuluka kwambiri ya chilekano tsopano, mokuti ife tikulitsogolera dziko lonse mu Amereka, mu milandu ya chilekano. Ife tikutsogolera dziko lonse. Kuli zilekano zochuluka kuno kuposa kwina kulikonseko, fuko lino, ndipo liyenera kukhala liri, ndipo limaganiziridwa ngati, fuko la Chikhristu. Ndi chotonzo bwanji, bwalo lathu la milandu ya chilekano! Ine ndikuganiza, chifukwa chake, ndi chifukwa chakuti amuna apita kutali ndi Mulungu, ndipo akazi apita kutali ndi Mulungu.

⁴⁹ Ndipo ife tikupeza, kuti, ngati mwamuna apemphera ndi mkazi akapemphera pa nkhaniyo; osati kungoyang'ana pa maso awiri okongola, kapena mapewa aakulu amphamvu, kapena zonga izo, kapena zokonda zina za chidziko; koma akanati ayang'ane poyamba kwa Mulungu, ndi kuti, “Mulungu, kodi ili ndi dongosolo Lanu?”

⁵⁰ Ine ndikuganiza, lero, pali kunamiza kochuluka kwambiri, basi monga mu sukulu. Pamene—pamene ana abwera cha apo, mmawa, ana ochuluka a kwa oyandikana nawo, a—abwenzi a ine awo, amabwera cha apo ndi kuti, “M'bale Branham, kodi inu mungatipempherere ife? Ife tiri ndi m—mayeso lero. I—ine ndagwira ntchito usiku wonse, ndipo ine sindikuwoneka kuti ine ndinga—ndingakhoze kukapeza izo mokhazikika. Mundipempherere ine.” Ine ndikuganiza kuti mwana wa sukulu aliyense, ngati inu muti, ngati... Ndipo makolo pa tebulo mmawa, inu mukanati. Muziti, “Amayi, John ali ndi mayeso lero. Tiyeni timupempherere iye tsopano.” Ine ndikuganiza izo zikanakhala zonse zomwe inu mukanakhoza konse kuzichita mwa njira ina iliyonse, kapena kukasuzumira pa pepala la winawake ndi kubela. Ine ndikuganiza ngati inu mukanangobwera poyera ndi kupempherera pa vutolo.

⁵¹ Ndipo ngati ife tikanati tiphunzire zomwe ife tikuchita pamene ife tikuti tikwatire, pamene ife tisankha mkazi wathu, mwamuna wathu, ngati ife tikanati tiziphunzire izo bwino! Mwamuna ayenera kumapemphera modzipereka, pakuti iye akhoza kuwononga moyo wake wonse. Kumbukirani, lumbirirolo liri “mpaka imfa mpomwe ife tidzalekana,” ndipo iye akhoza kuwononga moyo wake pa kupanga kusankha kolakwika. Koma ngati iye adziwa pamene, iye akupanga kusankha kolakwika ndipo iye akukwatira mkazi yemwe sali kuyenera kuti akhale mkazi wake, ndipo iye akuzichita izo mulimonse, ndiye ndi kulakwitsa kwake. Ngati mkazi amutenga mwamuna ndi kumadziwa kuti iye si woyenera kuti akhale

mwamunako kwa iwe, ndiye uko ndi kulakwitsa kwako komwe, iwe utadziwa kale chomwe chiri cholondola ndi cholakwika. Kotero, inu musamachite izo mpaka inu mutazipempherera bwino bwino.

⁵² Zomwezo zimagwiritsidwa ntchito pa kusankha mpingo. Tsopano, inu muyenera kumapempherera pa mpingo umene inu muli kusunghanamo. Kumbukirani, mipingo imanyamula mzimu.

⁵³ Tsopano, ine sindikufuna kuti ndikhale wotsutsa. Koma ine ndikuzindikira kuti ndine bambo wachikulire, ndipo ine ndiyenera kuti ndidzachoke kuno, limodzi la masiku awa. Ine ndiyenera kudzayankha pa Tsiku la Chiweruzo pa zomwe ine ndikuzinena usikuuno kapena nthawi ina iliyonse. Ndipo ine, kotero, ine ndiyenera kuti ndikhale wotsimikiza mwakufa ndi wokhuzidwa kwathunthu.

⁵⁴ Koma, inu mukapita mu mpingo, ndipo ngati inu mungapenye khalidwe la mpingo umenewo, inu mungomupenya m'busayo kanthawi, ndipo inu kawirikawiri mudzapeza kuti mpingo umachita monga m'busayo. Nthawizina, ine ndimadabwa ngati ife sitimangotengerana mzimu wa wina ndi mzake mmalo mwa Mzimu Woyera. Inu mukafika pa malo pomwe m'busa ali wachikhazikitso kwenikweni ndi wopitiriza, inu mudzapeza kuti osonkhana ali a njira yomweyo. Ine ndikubweretsani inu ku mpingo kumene ine ndikuwona abusa akuima ndi, kumagwedeza mitu yawo mmbuyo ndi mtsogolo. Inu mudzawapenye osonkhanawo, iwo amachita chinthu chomwecho. Inu mumutenge m'busa yemwe amangomezeka chirichonse, kawirikawiri mpingowo umachita chinthu chomwecho. Kotero, ngati ine ndikanakhala ndikusankha mpingo, ine ndikanati ndisankhe mpingo weniweni, wachikhazikitso, wa Uthenga Wathunthu, wa Baibulo, ine ndikanakhala ndikusankha wina woti ndiyikemo banja langa. Sankhani. Ine ndinayang'ana . . .

⁵⁵ Anyamata, tsiku lina, mwana wa M'bale Shakarian ndi mpongozi wawo, ananditengera ine kumtunda kuno kuti ndizampempherere mnyamata, woyimba, mnyamata wabwino. Anali atangobwerera . . . Fred Barker, limenelo linali dzina lake, anali atangobwerera kuchokera ku ulendo wake. Ndipo iwo anandiitana ine, nati, "Fred anali kufa." Ndiyeno, ine ndisanafike ku nyumbayo, uthenga wina unabwera, "Iye akhoza kukhala atafa pakali pano." Ndipo iye anati iye anali ndi—kuwukha magazi mu ubongo, ndipo iye anachititsidwa dzanzi, n—ndipo iye anali akufa, mkazi wake ankafuna ine kuti ndimupempherere iye.

⁵⁶ Ndipo ine ndinaganiza, "O, ngati ine nditi ndiyesere kuwuluka, iye akakhala atafa ine ndisanakafike uko, ndipo mwinamwake wafa panopo." Kotero, ine ndinaimba

mwamsanga ndipo ndinamupeza dona wamng'onoyo pa fonu. N—ndipo ife tinalumikizitsa foniyu, ndi ku khutu la Fred. Iye sankakhoza kumeza. Iwo anali akumupatsa kumeza kochita kuikirira. Ndipo pamene ife tinamupempherera iye, iye anati, anasonyeza, achichotse icho pa mmero pake. Iye amakhoza kumeza. Madokotala sanali kukhulupirira izo. Iwo anachichotsa icho, ndipo iye ankakhoza kumeza. Iye anali atakhala apo, tsiku lina.

Mpingo; kusankha mpingo.

⁵⁷ Kuitana kwa fonu kunangobwera, kanthawi kapitako, mmawa uno. Membala wa mpingo wanga, yemwe ali kwenikweni mkazi wa Chibaptisti wochokera ku Louisville, iye anamwalira molawirira mmawa uno. Ndipo mpingo wanga kwathuko, gulu lenileni la amuna odzipereka, anadzisonkhanitsa okha palimodzi ndipo anapita uko, osamalira thupi asanamukonze iye, anaima pa iye, napemphera mpaka moyo unabwerera mwa iye. Ndipo iye ali moyo, usikuuno. Akulu a mpingo wanga, chifukwa, iwo akhala akuphunzitsidwa kuti azikhulupirira kuti zinthu zonse ndi zotheka, kubwera kwa Mulungu modzipereka.

Kotero, inu muyenera muzipanga kusankha koyenera.

⁵⁸ Kachiwiri, mtundu wa mkazi yemwe mwamuna angamusankhe, adzanyezimiritsa zokhumba zake ndi khalidwe lake. Ngati mwamuna asankha mkazi wolakwika, izo zimanyezimiritsa khalidwe lake. Ndi komwe iye amazimangiriza, mwiniwakeko kumasonyeza moona zomwe ziri mwa iye. Mkazi amanyezimiritsa zomwe ziri mwa mwamunayo pamene iye amusankha iye kukhala mkazake. Izo zimasonyeza chomwe chiri pansu mkati mwake. Ziribe kanthu zomwe iye anena kunjaku, penyani chimene iye akwatira.

⁵⁹ Ine ndikapita ku ofesi ya munthu, ndipo iye nkumati ndi Mkhristu; zopachikaponse kuzungulira mmakoma, nyimbo zakale za kwasakwasa zija zikupitirira. Ine sindimasamala chimene iye anena. Ine sindimakhulupirira umboni wake, chifukwa mzimu wake umadyerera pa zinthu za mdziko izo. Chiani, titi, ngati iye akanati akwatire msungwana wa makolasi, kapena bwanji ngati iye akanakwatira ngenge yodziwa chiwerewere, kapena ricketta wokongola wamakono basi? Izo zimanyezimiritsa. Izo zimasonyeza zomwe iye ali nazo mu malingaliro ake, cha chomwe banja lake la mtsogolo liti lidzakhale, chifukwa iye wamutenga iye kuti alerere ana ake naye. Ndipo chirichonse chomwe iye ali, ndi momwe iye ati adzawalerere ana amenewo. Kotero, izo zimanyezimiritsa zomwe ziri mwa mwamunayo. Mwamuna yemwe amamutenga mkazi monga choncho, zimasonyeza basi zomwe iye akuganiza pa za tsogolo.

⁶⁰ Kodi inu mukanalingalira Mkhristu kuchita chinthu monga choncho? Ayi, bwana. Ine sindikanakhoza. Mkhristu woona sangati afunefune ngenge zokongola choterozo, ndi asungwana amakolasi, ndi ngenge zodziwa chiwerewere. Iye akanafunafuna khalidwe la Chikhristu.

⁶¹ Tsopano, inu simungakhoze kukhala nazo zinthu zonse. Pakhoza kukhala msungwana mmodzi yemwe ali wokongola kwenikweni. Ndipo msungwana winayo, mwinamwake iye... thunthu lake amawoneka bwinoko kuposa uyuyu. Ndipo inu mwina mungachite kuperekera nsembe wina pofuna mzakeyo, koma, ngati iye sali thunthu la dona, la mkazi. Ndipo, iye, ine sindikusamala ngati iye ali wokongola kapena ayi. Inu kuli bwino muyang'ane pa khalidwe lake, ngakhale iye ali wokongola kapena si wokongola.

⁶² Tsopano, pakuti, izo ndi zoyenera, ngati Mkhristu akanati asankhe mkazi, iye amayenera kumusankha mkazi weniweni, wobadwa-kachiwiri, mosasamala momwe iye amawonekera. Ndi chomwe iye ali, chomwe chimamupanga iye. Ndiyeno, kachiwiri, izo zimanyezimiritsa khalidwe lake lomwe laumulungu, ndipo zimanyezimiritsa zomwe ziri mu malingaliro ake ndi zomwe ziti zidzakhale mtsogolo, pakuti banja lake lidzaleledwa ndi mkazi woteroyo, kwa dongosolo lamtsogolo la banja lake.

⁶³ Ngati iye akwatira mmodzi wa maricketta amakono awa, ngenge zodziwa chiwerewere, kodi iye angayembekezere chiani? Kodi ndi banja la mtundu wanji lomwe mwamunayo angayembekezere kudzakhala nalo? Ngati iye akwatira msungwana yemwe alibe makhalidwe okwanira pa iye kuti azikhala pakhome ndi kumasamalira panyumba, ndipo akufuna kuti azikagwira ntchito mu ofesi ya winawake, kodi iye adzakhala wosamalira nyumba wa mtundu wanji? Inu mudzayenera kumakhala ndi olera ana ndi china chirichonse. Zoon.

⁶⁴ Tsopano, ine sindiri mochuluka wokonda zamakono izi, za akazi kumagwira ntchito. Pamene ine ndimawawona akazi awa atavala maunifolomu awa, atakwera nazungulira mu mzinda uno, pa njinga zamoto, ngati apolisi, ndi chamanyazi kwa mzinda uliwonse umene ungaloleze mkazi kuti azichita zimenezo. Mwaona? Mwaona? Pamene amuna ambiri sali pa ntchito, izo zimasonyeza kuganiza kwamakono kwa mzinda wathu. Izo zimasonyeza kutsika. Ife sitikusowa kuti tizikhala ndi akazi awo kunja uko monga choncho. Iwo alibe ntchito ayi kunja uko monga choncho.

⁶⁵ Pamene Mulungu anamupatsa mwamuna mkazi, Iye anamupatsa iye chinthu chopambana chimene Iye akanamupatsa iye, kunja kwa chipulumutso. Koma pamene wina apita nakayesera kuti azitenga malo a amuna, ndiye iye ali

pafupi chinthu choipisitsa chimene iye angachipeze. Tsopano, uko nkulondola. Mwaona?

Tsopano ife tikhoza kuwona kachitidwe kauzimu.

66 I—ine ndikudziwa izo nzoipa, inu mukuganiza kuti ndi zoipa, koma ndi Choonadi. Ife sitikusamala momwe izo ziriri zoipa, ife tiyenera kukomanizana nacho choona. Ndicho chimene Baibulo limaphunzitsa. Mwaona?

67 Tsopano, ife pano tikuwona mwapoyera dongosolo lauzimu, la Mulungu kukonzekera Banja Lake la mtsogolo ndi Mkwatibwi Wake wamtsogolo, akubwera powonekerayu tsopano.

68 Ngati mwamuna akwatira ngenge yodziwa chiwerewere, inu mumaona chimene iye akuchifuna mtsogolomo. Ngati mwamuna akwatira mkazi yemwe sangakhale pakhomo, inu mumaona chimene iye akuchiyembekezera mtsogolomo. Ndipo ine nthawi ina . . .

69 Izo zimveka mosakhala bwino. Ine ndikungomverera kuti ndizinene izo. Ndipo i—ine, kawirikawiri, ngati ine ndimverera kuti ndinene chinthucho. Ine ndimayenera kuti ndichinene icho. Ndipo kawirikawiri ndi njira ya Mulungu.

70 I—ine ndinkapita limodzi ndi mwini ziweto yemwe ine ndinkagwira naye ntchito, kukagula ng’ombe. Ndipo ine ndinazindikira munthu wachikulireyo nthawizonse ankayang’ana mu nkhope momwe mwa ng’ombe yaikazi asanapite kukaigula. Ndiye iye ankaitembenuza mutu wake, ndi kuiyang’ana mmbuyo ndi mtsogolo. Ine ndinkamutsatira iye limodzi, ndinkamupenyetsa iye. Ndipo iye ankaiyang’ana iyo chokweza ndi chotsitsa, ngati iyo imawoneka bwino bwino, thunthulo. Ndiye iye ankapotoloka ndi kukaiyang’ana iyo mu nkhope, ndipo nthawizina iye ankagwedeza mutu wake ndi kuyenda nachokapo.

Ine ndinati, “Jeff, ine ndikufuna kuti ndikufunse iwe chinachake.”

Iye anati, “Nena, Bill.”

71 Ndipo ine ndinati, “Chifukwa chiani inu nthawizonse mumaiyang’ana ng’ombeyo mu nkhope?” Ine ndinati, “Iyo ikuwoneka yabwino bwino, ng’ombe yabwino—yolemera bwino.”

72 Anati, “Ine ndikufuna kuti ndikuuze iwe, mnyamata, iwe uli ndi zochuluka zoti uziphunzire.” Ndipo i—ine ndinazindikira izo iye atandiiza ine kaye. Anati, “Ine sindikusamala momwe iyo inapangidwira. Iyo ikhoza kukhala ili yanyama, mpaka kufika ku mapazi. Koma ngati iyo ili ndi mayang’anidwe olusa awo mu nkhope yake, iwe usamaigule konse iyo.”

Ndinati, “Chifukwa chiani chomwecho, Jeff?”

⁷³ “Chabwino,” anati, “Chinthu choyamba ndicho,” anati, “iyo siimadzakhala phee konse.” Ndipo iye anati, “Chinthu chotsatira ndicho, iyo siidzakhala konse mayi kwa ana ang’ombe ake.” Ndipo anati, “Iwo ayiika iyo mukhola tsopano, nchifukwa chomwe iyo ili yonenepa. Iwe ukakayimasula iyo, ili ndi kuyang’ana kolusa uko, iyo ikadzithamangitsa yokha mpaka kufa.”

⁷⁴ Ine ndinati, “Inu mukudziwa, ine ndikukhala ngati ndaphunzira chinachake. Ine ndikukhulupirira izo zingagwiritsidwe ntchito kwa akazi, nawonso.” Kulondola. Kulondola.

⁷⁵ Kuyang’ana kolusa uko, kwa uricketta, ndi bwino ukhale kutali ndi iye, mnyamata, zinthu zonse za buluu izo pamwamba pa maso ake. Ndipo ine sindikanati. . . Ine sindikanazifuna izo. Ine sindikuganiza kuti izo ndi zoyenera kwa Mkhristu. Ine sindikusamala kuchuluka kwa momwe televizioni ndi pepala zikunenera kuti izo ndi zokongola. Awo ndi mawonekedwe oyipa, owopsyesetsa powaona omwe ine ndinayamba ndawawonapo mu moyo wanga.

⁷⁶ Pamene ine ndinaziwona izo choyamba, kuno ku cafeteria ya a Clifton, mmawa wina, pa kadzutsa. Ine ndinawaona ena, madona aang’ono awo akubwera. M’bale Arganbright anali atangobwera umo, ndi ine. Ndipo iye anali atapita ku zipinda zapansi. Ine ndinkayang’ana, ndipo msungwana ameneyo analowa umo. Ine ndinaganiza, “Chabwino, i—i—ine sindikudziwa.” Ine sindinayambe ndaziwonapo izo kale. Uwo unali mtundu winawake. O, izo zinkawoneka ngati iye anali ndi matenda, inu mukudziwa, basi kukhala ngati mawonekedwe-oseketsa. Ine sindikunena izo kuti ndikhale woseketsa. I—ine ndikunena izo. Inu mukudziwa, ine ndaliwonapo khate. Ndine mtumwi. Ine ndawonapo mitundu yonse ya kupunduka, inu mukudziwa ya momwe matenda. Ndipo ine ndinkati ndiyende kupita kwa dona wamng’ono ndi kukamuuya iye, “I—i—ine ndi mtumiki. I—ine ndimapempherera odwala. Kodi—kodi inu mungafune kuti ine ndikupemphereni inu?” Ndipo ine ndinali ndisanawone chirichonse chonga izo. Ndiyeno, apa panadza awiri kapena atatu ena, mkati. Ine ndinakhala ngati ndinabwerera mmbuyo ndiye ndipo ndinayembekezera.

⁷⁷ Ndipo M’bale Arganbright anabwera apo, kotero ine ndinati, “M’bale Arganbright?” Iye mwina akhoza kukhala ali pano. Ine ndinati, “Chavuta nchiani ndi mkazi uyo?” Mwaona?

Ndipo iye anati, “Uwo, uwo ndi utoto.”

⁷⁸ Ine ndinati, “Chabwino, mai, mai!” Mwaona? Ine ndimaganiza iwo amayenera kuti akamuike iye mu nyumba inayatizilombo kwina awake, inu mukudziwa, kuletsa izo kuti zingafalikire ponseponse kwa akazi ena.

⁷⁹ Koma, inu mukudziwa, inu muyenera kukonzekera, kuyang'ana, kupemphera, pamene inu mukusankha. Pakuti, ife tikuwona, ndi izi, Mawu a lonjezo. Iye, mkwatibwi yemwe mwamuna angati amusankhe, adzanyezimiritsa khalidwe lake. Izo zimanyezimiritsa chomwe chiri mwa iye.

⁸⁰ Tsopano, kodi inu mungakhoze kulingalira munthu, wodzazidwa ndi Mzimu Woyera, kutenga chinachake chonga icho kuti chikhale mkazake? [Osonkhana ati, “Ayi.”—Mkonzi.] I—i—ine sindikuziwona basi izo, m'bale. Tsopano, mwinamwake ine ndangokhala chidempete chakale. Koma, inu mukudziwa, i—ine sindingakhoze basi kuzimvetsa izo, onani, zindikirani, pakuti izo zidzanyezimiritsa chomwe chiri mwa iye. Iye ndi woti adzamuthandizire iye kupanga banja lake la mtsogolo.

⁸¹ Tsopano, ndiye, pamene ife tisintha kupita mmbuyo tsopano mu mphindi, kupita ku mbali yauzimu. Ndipo pamene inu muwuona mpingo umene uli mu dziko, ukuchita monga dziko, kumayembekezera za mu dziko, kumachita nawo za mdziko, kumawerengera malamulo a Mulungu ngati kuti Iye sanawalembe konse Iwo, ndiye i—inu mukhoza kungolingalira Khristu sadzatenga Mkwatibwi woteroyo. Kodi inu mungakhoze kulingalira kuutenga mpingo wamakono wa lerowu kukhala Mkwatibwi? Osati Ambuye wanga. Ine sindiri...Ine sindingakhoze nkomwe kuziwona izo. Ayi. Kumbukirani, tsopano, mwamuna ndi mkazake ali mmodzi. Kodi inu mukanadziphatikiza nokha kwa munthu wonga uyo? Ngati inu mungatero, izo ndithudi zingakhale ngati zikhumudwitse chikhulupiriro changa mwa inu.

⁸² Ndipo, ndiye, nanga bwanji Mulungu kudzilumikiza Yekha kwa chinachake chonga icho, wachiwerewere chachipembedzo mwachizolowezi? Inu mukuganiza Iye akanachita izo, “Ali nawo mawonekedwe aumulungu koma kumakana mphamvu yakeyo”? Iye sakanati achite konse izo. Iye ayenera kukhala nalo khalidwe Lake mwa iye. Mpingo weniweni, wobadwa-kachiwiri moona uyenera kukhala—ndi khalidwe limene linali mwa Khristu, chifukwa mwamuna ndi mkazake ali mmodzi. Ndipo ngati Yesu ankachita kokha izo zomwe zinkamukondweretsa Mulungu, ankasunga Mawu Ake ndipo ankawawonetsera Mawu Ake, Mkwatibwi Wake adzayenera kukhala ali wa mtundu womwewo wa khalidwe. Iye sakanakhoza, mwa njira iliyonse, kukhala chipembedzo. Chifukwa, ndiye, ziribe kanthu momwe inu mukufuna kunena kuti, “ayi,” iye amalamulidwa ndi gulu kwinakwake, lomwe limamuza iye choti achite ndi chimene iye sangakhoze kuchichita, ndipo, nthawi zambiri, mailosi milioni zitachoka ku Mawu owona.

⁸³ Izo ndi zoipa kwambiri kuti ife tinachoka konse kwa Mtsogoleri weniweni yemwe Mulungu anatisiyira ife kuti aziutsogolera Mpingo. Iye sanatumize konse woyang'anira wa dzikolo. Iye sanatumize konse mabishopu, makadinolo,

ansembe, mapapa. Iye anatumiza Mzimu Woyera kwa Mpingo, kuti uziutsogolera mpingo. “Pamene Iye Mzimu Woyera adzadza, Iye adzakutsogolerani inu mu Choonadi chonse, kuululira zinthu izi kwa inu, zomwe ine ndakuuzani inu, kuzibweretsa ku kukumbukira kwanu ndipo uzidzakusonyezani inu zinthu zomwe ziri nkudza.” Mzimu Woyera unali woti uzidzachita zimenezo. Tsopano, mpingo wamakono umadana nazo Izo. Iwo samazikonda Izo, kotero kodi iye akanakhoza bwanji kukhala Mkwatibwi wa Khristu? Anthu, lero akusankha, chipembedzo chamakono. Chomwe izo zimachita, izo zimanyezimiritsa kokha kumvetsa kwawo kosauka pa Mawu.

⁸⁴ Ine sindikutanthauza kuti ndipweteke, koma ine ndikutanthauza kuti ndizilole izo zizame mwakuya kokwanira mpaka inu muziyang’ana pa izo.

⁸⁵ Ine ndakwatitsapo mabanja angapo, koma izo nthawizonse zimandikumbutsa ine za Khristu ndi Mkwatibwi Wake. Chimodzi cha zikwati chomwe ine ndinachichita kuno, nthawi ina pakale, i—icho chinali ndithu chinthu chosaiwalika mu moyo wanga. Izo zakhala ziri zaka zingapo zitapitapo, pamene ine ndinali mtumiki wamng’ono basi.

⁸⁶ M’bale wanga anali kugwira ntchito k—ku P.W.A. Ine sindikudziwa ngati aliyense amaikumbukira konse iyo, panobe, kapena ayi, aliyense yemwe ali wamkulu monga ine. Ndipo iyo inali—ntchito yomwe boma linali nayo. Ndipo m’bale wanga ankagwira ntchito, pafupi mailosi sate. Iwo anali kukumba madamu ena, ntchito ya kosungira.

⁸⁷ Ndipo uko kunali mnyamata ankagwira ntchito kumeneko, ndi iye, wochokera ku Indianapolis, pafupi, o, pafupi mailosi handiredi kumtunda kwa Jeffersonville kumene i—ine ndimakhala, kapena ndinkakhala. Ndipo uko kunali... Iye ananena kwa M’bale wanga, tsiku lina. Iye anati, “Doc,” iye anati, “I—ine ndikufuna... ine ndikuti ndikwatire, ngati ine ndikanangokhala nazo ndalama zokwanira kuti ndimulipire mlaliki.” Iye anati, “I—ine ndiri nazo ndalama zokwanira kuti ndipeze lainsesi yanga, koma,” anati, “Ine ndiribe ndalama zokwanira zoti ndimulipire mlaliki.

⁸⁸ Doc anati, “Chabwino, m’bale wanga ndi mlaliki, n—ndipo i—iye akhoza kukukwatitsa iwe.” Iye anati, “Iye samawalipiritsa konse anthu pa zinthu zonga izo.”

Iye anati, “Kodi iwe ungakamufunse iye ngati iye angandikwatitse ine?”

⁸⁹ Chabwino, usiku umenewo m’bale wanga anandifunsa ine. Ine ndinati, “Ngati iye sanakwatirepo konse kale, aliyense wa iwo, ndipo chirichonse chawo chiri bwino.” Iye anati, chabwino, iye akamufunsa iye. Ndipo ine ndinati, “Ngati izo ziri, kamuuze iye, abwere kuno.”

⁹⁰ Kotero, pamene Loweruka linabwerapo ndipo mnyamatayo anabwera kuno. Chakhala chiri chinthu chachikulu kwa ine, kuti nthawizonse ndiziyang'ana mmbuyo pa izi. Ine . . . Madzulo amvula, ndipo galimoto yakale ya Chevrolet, ili ndi nyali zitamangiriridwa ndi mawaya a mabelo, yomwe inayenda, kufika pakhomopo. Kanali kanthawi ine nditangotaya mkazi wanga, ndipo ine ndinali kukonza, zipinda ziwiri zazing'ono. N—ndipo Doc anali kuntunda uko ndi ine, tikuwayembekezera iwo.

⁹¹ N—ndipo mnyamatayo anatuluka mu galimotoyo, ndipo iye ndithudi sankawoneka ngati mkwati, kwa ine, kapena momwe akanachitira kwa aliyense, ine ndikulingalira. Eya. Ine ndikhoza pafupi. . . kugula nsapato zabwino, kwa dola ndi hafu. Ndipo iye anali atavala zake zoti zinapondedwapo. Ndipo thalauza yake inalidi mwathumba. Ndipo iye anali atavala chimodzi cha zikhoto zachikale za chikopa cha nungu. Ine sindikulingalira ena a inu anthu achikulire mungazikumbukire. Icho chinkawoneka ngati icho chinali chitazunguzidwa mu makina ochapira chopanda kusitidwa, ndi icho chinali chokwinyika, ndi chomangidwira mmwamba monga *chonchi*, ndi ngodyayo ili mmwamba.

⁹² Ndipo—dona wamng'onoyo anatulukira ku mbali, ali ndi yaing'ono, o, madiresi ena awo achikale amandalasi.

⁹³ Ine sindikudziwa. Ine ndinapanga kulakwitsa potchula mtundu uwo wa nsalu, nthawi ina. Gingham, ine ndikukhulupirira iyo imatchedwa. Ndipo kotero iyo inali. . . Ine ndanena izo molakwika kachiwiri. I—ine nthawizonse ndimachita choncho. Ndipo ine ndinati. . .

⁹⁴ Iye anatuluka mu galimotoi, ndipo iwo anabwera pamwamba pa masitepewo. N—ndipo pamene iwo ankalowa umo, kanthu kakang'ono kosaukako, iye. . . ine ndikulingalira, iye, basi zonse zomwe iye anali atavala inali siketiyo. Ndipo iye sanali atavala nsapato, nkomwe. Iye anali atakwera matola kuchokera ku Indianapolis, pobwera. Anali ndi tsitsi laling'ono likulendewera pansu, kumbuyo, lalitali, lokhala ngati mangongo ofika pansu ku nsana wake. Ankawoneka wamng'ono kwambiri.

Ndipo ine ndinati kwa iye, “Kodi ndiwe wamkulu mokwanira kuti ukwatiwe?”

⁹⁵ Iye anati, “Inde, bwana.” Ndipo iye anati, “Ine ndiri ndi chilolezo changa cholembedwa kuchokera kwa bambo anga ndi amai.” Iye anati, “Ine ndimayenera kukachisonyeza icho—ku khoti kuno, kuti ndipeze laisensi yanga.”

⁹⁶ Ine ndinati, “Chabwino.” Ine ndinati, “Ine ndikanakonda kuti ndiyankhule kwa inu pang'ono pokha ife tisanachite chikwati ichi.” Iwo anakhala pansu. Mnyamatayo anapitirira kuyang'ana ponse ponse mchipindamo; anali wosowa kumetedwa tsitsi kwambiri ndithu. Iye anapitirira kuyang'ana ponseponse m'chipindacho. Iye sanali kumvetsera kwa ine. Ine

ndinati, “Mwananga, ine ndikufuna kuti iwe uzimvetsera ku zomwe ine ndikunena.”

Anati, “Inde, bwana.”

Ndipo ine ndinati, “Iwe ukumukonda msungwana uyu?”

Iye anati, “Inde, bwana. Ine ndikutero.”

Ine ndinati, “Iwe ukumukonda iye?”

“Inde, bwana. Ine ndikutero.”

⁹⁷ Ine ndinati, “Tsopano, kodi iwe uli nawo malo oti umutengereko iye iweyo pambuyo pa kumukwatira?”

Anati, “Inde, bwana.”

⁹⁸ Ine ndinati, “Chabwino. Tsopano,” ine ndinati, “ine ndikufuna kuti ndikufunse iwe chinachake. Ine ndamva, iwe ukugwira ntchito ku mtunda kuno ku P.W.A iyi.”

Ndipo iye anati, “Inde, bwana.” Ndi ya pafupi madola thwelofu pa sabata.

Ine ndinati, “Iwe ukuganiza iwe ukamukhalitsa moyo iye?”

Iye anati, “Ine ndikachita zonse zomwe ine ndingakhoze kuzichita.”

⁹⁹ Ndipo ine ndinati, “Chabwino, izo zonse ziri bwino.” Ndipo ine ndinati, “Tsopano, bwanji ngati itamuthera. . . Bwanji ngati iye atamuchotsa ntchito iyi, mlongo? Kodi iwe udzachita chiani, udzathawira kwanu, kwa amai, ababa?”

Iye anati, “Ayi, bwana. Ine ndidzakhala ndiri naye.”

¹⁰⁰ Ndipo ine ndinati, “Bwanji, bwana, ngati inu mutakhala nao ana atatu kapena anai, opanda choti muziwadyetsa iwo, ndipo inu mulibe ntchito iliyonse. Kodi inu mudzachita chiani, kumutumiza iye achoke?”

¹⁰¹ Anati, “Ayi, bwana. Ine ndidzavutikira mopitirirabe. Ife tidzakwanitsa izo, mwa njira yina.”

¹⁰² Ine ndinamverera kuchepa. Ndipo ine ndinawona kuti iye ankamukonda iye kwenikweni, ndipo iwo anakondana wina ndi mzake. Ine ndinawakwatitsa iwo.

¹⁰³ Ndiye ine ndinkadabwa komwe iye anamutengera iye. Mu masiku angapo, ine ndinamufunsa m'bale wanga, Doc, kumene uko kuli. Iye anati, “Inu mudzapite ku New Albany,” mzinda wawung'ono kumusi kwathuku.

¹⁰⁴ Ndipo kumusi kwa mtsinjewo, kumene ine ndinali ndi malata nditawaunjika, kumene ine ndinkapita tsiku lililonse pamene i—ine ndinali woyang'anira mawayaya. Koteru pamene anthu ena onsewo, awo onse ankakhala apo, kumanena nthabwala ndi zinthu, ine ndinkakhoza kulowa mu galimoto ndi kuthamangira ku mtsinjeko ndi kukapemphera pa nthawi iyo! . . . ? . . . Ndi kuwerenga Baibulo langa, pansu pa chidutswa

chachikulu cha malata kumene kunali ntchito za zitsulo kale. Kuli gulu la magalimoto akale abokosi omwe ali kumeneko.

¹⁰⁵ Ndipo mnyamata uyu anali atapita kumeneko ndipo anakatenga imodzi ya magalimoto abokosi amenewo ndipo anadzichekera chitseko cholowera mu iyo. Ndipo anali atatenga manyuzipepala ndi mabatani achitake.

¹⁰⁶ Ndi angati akudziwa chomwe batani cachitake liri? Palibe aku Kentucky pano, ndiye. Ndizo, kutenga chidutswa cha chibolodi, kuika chikhomo mmenemo, katsatsa kakang'ono. Ndiyeno, nkukakankhira iko umo . . . Ndilo batani lachitake.

¹⁰⁷ Kotero, iwo anali ataziyika izo paliponse. Ndipo iye anali atapita uko kopanga zitsulo ndipo anakadzitengera zinthu zina, ndipo anadzapanga sitepe, kuti azikwerera umo. Ndipo anakatenga mabokosi ena akale, ndipo anadzipangira tebulo. Ndipo ine ndinaganiza, tsiku lina, "Ine ndipita kumeneko ndikawone momwe iwo akukhalira limodzi."

¹⁰⁸ Pafupi miyezi sikisi zisanachite izo, ine ndinakwatitsa mwana wamkazi wa a E.V. Knight kwa mwana wamwamuna wa a E.T. Slider. E.V. Knight, mmodzi wa amuna olemera omwe alipo pa Mtsinje wa Ohio, ndipo, o, amayendetsa mafakitare akulu konseko, amapanga nyumba zopangidwiratu izi, ndi zina zotero. Ndi—ndipo Slider, E.T. Slider, ndi kampani ya mchenga ndi miyala, ana a mamilionea. Ndipo ine ndinawakwatitsa iwo.

¹⁰⁹ Ndipo ine ndinkabwerera ku malowo, kumakaziphunzira izo kwa pafupi masabata awiri, ndi kumabwerera mu komangidwa ndi kumakagwada pa mtsamiro. Ndi zapamwamba zonse ndi chirichonse chomwe ine ndinayamba ndadutsamo, pafupifupi, ndinkayenera kuti ndidutse mu izo, kuti ndiwakwatitse awiri awo! Ndipo pamene iwo anatulukira, bwanji, iwo anali . . . Banja lina laling'ono ili linangoima pamenepo mu chipinda chaching'ono chachikale momwe ife tinali ndi ndalema wamng'ono ndi kama wopindidwa, koma iwo onse anakwatitsidwa ndi mwambo wofanana.

¹¹⁰ Ndiyeno, tsiku lina, ine ndinaganiza ndipite uko ndi kukalichezera banja lolemera ili. Iwo sankasowa kuti azigwira ntchito, makolo awo anali mamilionea, anali atawamangira iwo nyumba yabwino. Moona, E.V. Knight uyu, uko, kuno pa phirili, zigwiriro za zitseko zake ndi za fortini karati pa nyumba yake yachifumu yaikuluyo, kotero inu mukhoza kulingalira mtundu wa nyumba yomwe iwo anali kukhalamo. Iwo sankasowa kuti azigwira ntchito. Iwo ankakhala ndi Cadillac yabwino imapatsidwa kwa iwo chaka chirichonse. Ndi basi, ana okha, ndipo iwo anali nacho basi chirichonse chomwe iwo ankachifuna. Pamene ine ndinapita uko tsiku lina . . .

¹¹¹ Tsopano, momwe ine ndinadziwirana ndi iwo, mmodzi wa abwenzi awo anali bwenzi wabwino wa ine. Ife tonse timakhala ngati tinkakondana limodzi. Ndipo umo ndi momwe

ine ndinadziwirana nawo, pamene iwo anafuna kuti ine ndiwakwatitse iwo.

¹¹² Kotero ine ndinapita kukawachezera iwo. Ine ndinatuluka panjapo mu Ford yanga yakale, panjapo, ndipo ndinayenda kukwera pa masitepe. N—ndipo ine ndinafika apo, pang’ono ng’ono moyandikira, kwambiri, ndipo ine ndinawamva iwo. Ndipo iwo anali akukangana kwenikweni. Iwo amachitirana nsanje wina ndi mzake. Iwo anali atapita kovina. Iye anali msungwana wokongola kwambiri. Ndipo iye anali mtundu wa amodzi a ngenge zokongola izi. Iye anatenga mphoto zambiri cha kumeneko, ndipo anawina magalimoto ena ndi zinthu, chifukwa chokhala ngenge yokongola. Ndipo ine ndinayang’ana pa iwo, ndipo wina anali atakhala ku ngodya imodzi ndi wina ku imzake, akukangana za mnyamata wina yemwe iye anavina naye, kapena msungwana wina, chinachake.

¹¹³ Pamene ine ndinabwera apo, iwo analumpha mofulumira kwenikweni ndi kukumbatirana wina ndi mzake nadutsa, bwalolo, ndi awo—manja awo, kudutsa pa bwalolo, anabwera akuyenda molunjika ku khomo. Anati, “Bwanji, moni apo, M’bale Branham! Zikukuyenderani bwanji inu?”

Ndinati, “Ziri bwino. Zikukuyenderani bwanji inuyo?”

¹¹⁴ Ndipo, “O,” iye anati, “I—ine. . .Ndife okondwa kwambiri. Si choncho ife, wokondedwa?”

Ndipo iye anati, “Inde, wokondedwa.” Mwaona?

¹¹⁵ Tsopano, inu mukuona, inu mukungovala chinachake chomwe sichiri chenicheni. Tsopano, inu simungakhoze kutenthetsedwa ndi moto wopentedwa, monga mipingo ina iyi imayesera kupenta pentekoste, za chinachake chomwe chinachitika zaka zikwi zapitazo kapena zaka zikwi ziwiri zapitazo. Inu simungakhoze kutenthetsedwa ndi moto wopentedwa. Pentekoste ili basi yeniyeni lero momwe iyo inaliri apo. Mwaona? Eya. Moto udakali nkugwa. Iwo si moto wopentedwa. Iwo ndi Moto weniweni.

¹¹⁶ Kotero, iwo, basi apo iwo anali. Mukuona? I—ine sindikanafuna kumakhala monga choncho.

¹¹⁷ “O,” ine ndinaganiza, “inu mukudziwa, kungowoloka kakhwawa uko ndi kuoloka pa mtsinjewo, uko ndi kumene banja lina ili linakatsirizirako.” Ine ndinaganiza, “Loweruka lina madzulo ine ndizembera kumeneko ndi kukawona momwe iwo zikuwayendera.”

¹¹⁸ Kotero ine, wotuwa pa nkhope, ndipo nditavala ovulolo yakuda, nditavala zida zanga. Ine ndinaganiza, “Ine ndizembera kwa iwo.” Ine ndinazemberako, ngati kuti ndimayang’ana zotetezera magetsi ngati zang’ambidwa ndi mphezi kapena chinachake, ndipo pamene ine ndinkayenda motsatira mawaya a telefoni, nthambo za magetsi motsatira mtsinje. Ndipo apo

panali Chevrolet yakaleyo, inali ili kutsogolo komwe. Pafupi patapita chaka, ine nditawakwatitsa kale iwo. Ndipo apo panali a—a... Chitseko chinali chotseguka, ndipo ine ndimakhoza kuwamva iwo akuyankhula. Kotero izi zikumveka monga wachinyengo, koma ine ndinayenda moyandikira ndithu kuti ine ndikanakhoza kumvetsera, ndione zomwe iwo anali kunena. Ndinaima apo. Ndipo ine basi ndinkangofuna kuti ndidziwe, kwa ndekha.

119 Ine ndimakonda kufufuza kuti ndizikhala wotsimikiza pa zomwe ine ndimaziyanikhula. Umo ndi momwe ine ndimachitira nao Mawu a Mulungu. Kodi Iwo ali Choonadi, kapena Iwo si Choonadi? Kodi Iye asunga Mawu Ake, kapena Iye sawasunga Mawu Ake? Iye akati asasunge Mawu Ake, ndiye Iye si Mulungu. Mwaona? Iye akasunga Mawu Ake, Iye ndi Mulungu. Mwaona?

120 Ndipo kotero ine ndimafuna kuti ndiwone momwe iwo zinali kuwayendera. Ndipo ine ndinazembera motsatira mbaliyo, mophweka kwenikweni. Ine ndinamumva iye akuti, “O, wokonedwa, ine ndimafuna kuti ndikugulire imeneyo iwe, kwambiri ndithu.”

121 Iye anati, “Tsopano, taona, wokomamtima.” Iye anati, “Diresi iyi ili bwino.” Iye anati, “Moti, iyi ili bwino basi.” Anati, “Ine ndikuyamikira iyo. Koma iwe ukuona . . .”

122 Ine ndinazemba chapamenepo, chotero kuti ine ndikanakhoza kumayang’ana kupyolera mu mng’alu, kumene chitseko chinali chitakankhidwa motseguka apo mu galimoto yabokosiyo. Ndipo apo iye anali, atakhala mmenemo, ndi mkaziyo ali pa miyendo pake; ndipo nkono wamkaziyo mokumbatira iye, ndi nkono wake mokumbatira iye. Ndipo iye anali ndi chimodzi cha zipewa izi zakale zofewa, ndipo anali ataika bowo laling’ono, anachiphwanyira icho pansi, pamwambapo, ndipo anatsanuliramo za cheke chake cha malipiro, mmenemo. I—iye anali atachiika icho pa tebulo. Ankati, “Zochuluka *chotere* ndi za zakudya. Zochuluka *chotere* za inshuranshe. Ndi zochuluka *chotere* za galimoto.” Ndipo iwo sankakhoza kupangitsa kuti zikwanire. Ndinafika popeza kuti, iye anali ataiwona diresi yaing’ono uko pa zenera, anakhala akuyang’ana pa iyo kwa masabata angapo, yomwe inkagulitsidwa dola ndi chinachake. Iye ankafuna kuti akaigule iyo. Anati, “Chabwino, wokonedwa, iwe ungewoneke wokongola kwambiri mu iyo.” Ndipo iye anati . . .

123 Iye anati, “Koma wokonedwa, i—ine ndiri nayo diresi. I—ine sindikuisowa iyo kwenikweni.” Mwaona? Ndipo ngenge yaing’ono iyo . . .

124 Ine ndinabwerera mmbuyo, ndipo ndinayang’ana kumbuyo. Ine ndinkakhoza kuwona—nsanjayo pamwamba pa nyumba zina. Ine ndinaima pamenepo ndipo ndinayang’ana, maminiti angapo. Ine ndinaganiza, “Munthu wolemera ndi uti?” Ine

ndinaganiza, “Ngati, Bill Branham, ngati iwe ukufuna kuti utenge malo ati, iwe ukanafuna kupita kuti?” Kwa ine, ine sindikanatenga ayi chinthu chokongola icho pamwamba pa phirilo. Ine ndikanatenga khalidwe ili pansi pano, ngati womanga banja weniweni, winawake yemwe akanamandikonda ine ndi kumakhala nane, winawake yemwe angayesere kumanga banja; ndipo osati kulirira chirichonse, chifukwa cha zokongola; ndi winawake yemwe akanamakhala ndi iwe, gawo la iwe.

¹²⁵ Izo nthawizonse zandikanirira ine, momwe izo zinaliri. Mmodzi anasankha msungwana wokongola, winayo anasankha khalidwe. Tsopano, ndiyo njira yokha yomwe iwe ungakhoze kusankhira. Poyamba, funafuna khalidwe ndipo, kenako, ngati iwe ukumukonda iye. Chabwino.

¹²⁶ Zindikirani, Adamu woyamba wa Mulungu analibe kusankha kulikonse, kwa mkazi wake. Iye sanakhale ndi kusankha. Mulungu anangomupangira iye mmodzi, ndipo iye sanachite kumusankha iye. Koteri ife tikupeza kuti iye anamutsogolera iye mosochera kuchoka ku Mawu a Mulungu. Iye sanachite kupempherera pa nkhaniyo. I—i—iye sali monga inu ndi ine. Iye sanakhale ndi kusankha. Ndipo kachiwiri, pochita izo, iye anamutsogolera iye kuchoka pa malo ake olondola pokhala mwana wa Mulungu. Ndipo iye anachita izo pa kumusonyeza iye njira yamakono kwambiri ya kakhalidwe, chinachake chimene iwo kwenikweni sakanati achichite. Koma khalidwe la iye linasonyeza kuti iye anali kulakwitsa. Zolinga zake ndi zokhumba zinali zolakwika basi. Ndipo anamukakamiza iye, mwa kulingalira kwake, kuti kuwala kwatsopano kwamakono kumene iye anali atakupeza, zomwe zinali zotsutsana ndi Mawu a Mulungu, inali njira yabwinoko yokhalira moyo.

¹²⁷ Ndipo ndi akazi angati lero, ndi mosinthanitsa, amuna, omwe angakhoze kumukoka mkazi wabwino kumchotsa kwa Mulungu, kapena kumukoka mwamuna wabwino kumchotsa kwa Mulungu, pa kuyesera kumuza iye, “Chipembedzo ichi, iye mnyamata wachipentekoste! Chipembedzo icho,” iwo amati, “o, Icho chonse ncha kachitidwe-kachikale. Ndi chakale chautsi. Musati muzichikhulupirira Icho.” Inu kulibwino muzipemphera zolimba inu musanamukwatire msungwana ameneyo. Ine sindikusamala momwe iye aliri wokongola. Chinthu chomwecho kwa mwamuna.

¹²⁸ Iye anamukakamizira iye kuti achoke ku chifuniro cha Mulungu ndipo anamupangitsa iye kuti achite chinachake chimene iye sakanayenera kuti achichite, ndipo, ndi icho, anayambitsa imfa kwa mtundu wonse wa anthu. Nchifukwa chake Baibulo limamuletsa iye kuti aziphunzitsa, kapena kuti azilalikira, kapena kuchita ndi Mawu a Mulungu, mwa mtundu ulionse.

¹³⁷ Zindikirani, tsopano, iye sakanakhoza kukhala naye kupatula mwamuna mmodzi, chifukwa, “Mkazi anapangidwira kwa mwamuna, ndipo osati mwamuna kwa mkazi.” Akazi onse faifi handiredi aja anali basi mkazi wa Davide, ndipo icho chinali choimira. Pamene Khristu adzakhala pa Mpandowachifumu mu Zakachikwi, Mkwatibwi Wake sadzakhala ali munthu mmodzi, koma iwo adzakhala ali makumi a zikwi, Mkwatibwi, onse mwa Mmodzi. Ndipo Davide anali nao akazi ambiri, mwa payekha, koma kokha onse awo palimodzi anali mkazi wake. Monga Thupi lonse la okhulupirira liri Mkwatibwi wa Khristu, chifukwa Ali Iyeyo, mkazi. Iye anali Mwamuna. Tsopano, ife tinapangidwira kwa Khristu. Khristu sanapangidwire kwa ife.

¹³⁸ Ndi chimene ife tikuyesera kuti tizichita lero mu mabukhu athu owerenga, ndi kuyesera kumawapanga Mawu (omwe ali Khristu) azitiyenera ife, mmalo moti ife tiziyesera kudzipanga tokha kuti tiziyenera kwa Mawu. Ndiko kusiyana kwake.

¹³⁹ Pamene mwamuna asankha msungwana winawake kuchokera mu banja, iye sayenera kuti azidalira pa kukongola, pakuti kukongola ndi konyenga. Ndipo kukongola, kukongola kwamakono kwamdziko, ndi kwa Mdierekezi.

“O,” ine ndikumumva wina akuti kunjja uko, “khala wosamalira apa, mlaliki.”

¹⁴⁰ Ine ndikunena kuti zinthu izi za pa dziko lapansi lino, zomwe zimatchedwa kukongola, ziri mwamtheradi za Mdierekezi. Ine nditsimikizira izo kwa inu. Ndiye, mu kuwala kwa ndemanga iyi, tiyeni tifufuze Mawu oyera a Mulungu, kuti tiwone ngati izo ziri zolondola kapena ayi. Ndipo ena a akazi inu mumafuna kuti mukhale okongola kwambiri! Tione kumene izo zikuchokera. Pachiyambi, ife tikupeza kuti Satana anali wokongola kwambiri mpaka iye anawanyenga Angelo. Ndipo iye anali Mngelo wokongola kwambiri mwa onse a iwo. Zikusonyeza, iko kumagona mwa Mdierekezi. Miyambo imati, Solomoni anati, “Kukongola ndi kwachabe.” Ndiko kulondola. Tchimo ndi lokongola. Ndithudi, ilo liri. Ilo limakopa.

¹⁴¹ Ine ndikufuna kuti ndikufunsemi inu, ndi kunena chinachake apa kwa inu. Ine ndikufuna kuti inu muzindikire, miniti pang’ono. Mwa zolengedwa zonse mdziko, mbalame, nyama, ife tikupeza kuti pa moyo wazinyama, zonse kupatula anthu, ndi chachimuna chimene chiri chokongola, ndipo osati chachikazi. Bwanji ichoncho? Tayang’anani pa. . . Tayang’anani pa gwape, g—gwape wokongola wamkulu ali ndi nyanga zake, ndi gwape wamkazi wamng’ono wonga bulu. Tayang’anani pa t—thazi, nkhuuku yaing’ono, ya mangamanga, ndi tambala wamkulu wokongola nthenga. Tayang’anani pa mbalame yaimuna ndi mbalame yaikazi. Tayang’anani pa bakha wamphongo ndi wamkazi. Mwaona? Ndipo palibe cholengedwa chimodzi mu

dziko, chimene chinapangidwa, chimene chingakhoze kunyenga ndi kudzinnyadzitsa ngati mkazi.

¹⁴² Tsopano, mlongo, musati muime ndi kupita kunja. Ingodikirani mpaka ife timve mapeto a Izi. Mukuona? Mukuona?

¹⁴³ Palibe kanthu kena, palibe chachikazi pambali pa mkazi, chingakhoze kukhala chopanda khalidwe. Inu mumamutcha garu, “slut,” inu mumaitcha nkhumba “s—sow,” koma, mwamakhalidwe, izo ziri nao makhalidwe ochuluka kuposa theka la akatswiri apakanema omwe alipo kuno. Iwo sangakhoze kukhala chinthu chinachake koma akhalidwe.

¹⁴⁴ Ndipo mkazi anali yemwe anachita kusinthidwa, kuti azichita zosokonezeka. Ndiko kulondola. Mukuona kumene kukongola kumamutengera iye uko? Tsopano, ndicho chifukwa kuti, lero, ife tikupeza kuti akazi ali pa kuchuluka kwa kukongola. Inu mukamutenga Pearl Bryan, inu munayamba mwachiwonapo chithunzi chake? Ankayenera kukhala wokongola kwambiri wa Amereka. Palibe mwana wa sukulu wochokera ku sukulu iliyonse koma yemwe akanakhoza kumuika iye mu—mzere wa kumbuyo. Kodi inu mumadziwa kuti izo zimayenera kukhala mwanjira imeneyo? Kodi inu mumadziwa kuti Baibulo limayankhula kuti umo ndi momwe ziti zidzakhalire ziri?

¹⁴⁵ Kodi inu mukudziwa kuti kugwa kunabwera ndi akazi pa chiyambi? Ndipo kugwa... Mapeto adzathera mwanjira yomweyo, akazi kubwera mu ulamuliro ndi kumalamulira pa amuna, ndi zina zotero. Inu mukudziwa Lemba limanena zimenezo? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Inu mukudziwa, tsiku limene iye akuvala zovala za amuna, kumalidula tsitsi lake, zinthu zonsezo ndi zosiyana ndi Mawu a Mulungu. Ndipo inu mukudziwa iye akuimira mpingo? [“Inde.”] Pamene, inu mupenya chimene akazi akuchita, inu muwona chimene mpingo ukuchita. Ndizo ndendende kulondola. Tsopano, tsopano, izo basi ndi zoonza monga Mawu a Mulungu ali owona.

¹⁴⁶ Palibe chachikazi china chiri chopangidwa kuti chingadzinyazitse monga mkazi angakhozere. Ndipo apobe, kupyolera mu izo, poti anapangidwa kuchokera...

¹⁴⁷ Iye sanali mu kulenga koyamba. Zazikazi zina zonse ziri mu chirengedwe chapachiyambi: mbalame, yaikazi ndi yaimuna; zinyama, zamphongo ndi zazikazi. Koma, mu moyo waumunthu, Mulungu anangopanga mwamuna, ndipo Iye anatenga kuchokera kwa iye. Ndipo mkazi ndi chopangidwa kuchokera kwa mwamuna, chifukwa Mulungu sanayambitse chinthu choterocho. Fufuzani Malemba. Ndendende kulondola. Mulungu, ayi, bwana, mu kulenga Kwake kwapachiyambi. Iye anaikidwa kunja uko.

¹⁴⁸ Koma ngati iye angakhoze kudzigwira yekha molondola, ndi mphoto yaikulu bwanji yomwe iye ali nayo kuposa

mwamuna. Iye waikidwa pa malo oyesedwera. Kupyolera mwa iye kunabwera imfa. Iye ndi wolakwa pa imfa zonse. Komano Mulungu anatembenuka apo ndipo anamgwiritsa ntchito mmodzi kuti abweretsenso Moyo kachiwiri; anabweretsa Mwana Wake kupyolera mwa mkazi, womvera uyo. Koma yemwe ali woipa ndi w—woipitsitsa yemwe alipo; palibe chirichonse chingakhoze kukhala chotsika choncho.

¹⁴⁹ Kaini, mwana wake wa Satana, ankaganiza kuti Mulungu amalandira kukongola. Iye akutero lero. Kaini anali mwana wamwamuna wa Satana. “O, tsopano!” inu mukuti. Ife sitipita mwatsatane pa izo; koma ingondilolani ine ndikukhazikitsireni inu izo. Baibulo linanena kuti iye “anali wa woipa uyo.” Kotero, icho chikukhazikitsa izo. Chabwino. Tsopano, iye anali Mwana wa Satana. Ndipo iye ankaganiza kuti, kubweretsapo guwa ndi kulipanga ilo kukhala lokongola kwambiri pa kupembedza, ndi chimene Mulungu akanati achilemekeze.

¹⁵⁰ Iwo akuganiza, ganiza chinthu chomwecho lero. Ndithudi. Ichi, “Ife timange chinyumba chachikulu kwambiri. Ife tikhale ndi zipembedzo zazikulu. Ife timange chinyumba chachikulu kwambiri ndi anthu ovala bwino kwambiri, alaliki otukuka kwambiri.” Nthawizina Mulungu amakhala mailosi mamiloni khumi kwa izo. Uko nkulondola. Komabe, iwo ndi mpingo.

¹⁵¹ Kotero, ngati Mulungu amangolemekeza kupembedza, kudzipereka, nsembe, Kaini anali wolungama basi monga analiri Abele. Koma zinali mwa vumbulutso, kuti iye anamvetsa kuti sanali maapulo omwe makolo ake anadya.

¹⁵² Ine ndikuti ndinene chinachake pano chomwe sichimveka bwino kwa mtumiki, koma ine ndikuti ndichinene icho, mulimonse. Ine ndimawamva ena awa akunena zinthu, chotero amanena nthabwala zazing’ono. Ine sindikutanthauza izo. Ine ndinena izi, ngakhalebe, “Ngati kudya maapulo kunawapangitsa akazi kuzindikira kuti iwo anali maliseche, ife ndibwino tipereke maapulo kachiwiri.” Mukuona? Mukuona? A-nha. Ndikhululukireni ine chifukwa cha izo, koma basi chotero kuti zisintheko. Ine ndakumangirirani inu pano, pa kuyankhula za akazi, ndi zina zotero. I—i—ine ndikufuna kuti inu mumasuke kwa miniti, kwa chomwe chikubwera motsatira. Tsopano, zindikirani, inu. Iwo sanali maapulo. Ife tikudziwa izo.

¹⁵³ Mpingo wakhala mu masiku awa, ndi zozikwanitsa zake, monga zokwanitsidwa kupangidwa ndi anthu zina zonse, iwo ukukhala mwasayansi. Iwo akuyesera kuti apange mpingo wa mwasayansi, ndi kukopa kwa zithunzi ndi nsanja zazikulu. Ndipo ndi zoipa kwambiri kuti Achipentekoste alowa nawo mu chizolowezi chimenecho. Inu mukanakhala bwinoko muli ndi nkhotcho, kumusi uko pa ngodya, muli ndi Mzimu wa Mulungu pokuzungulirani inu. Ameni. Ndi zimenezo. Koma inu mukuyesera kuti muzidzifanizitsa ndi ena onse awo, chifukwa

inu mwakhala chipembedzo. Ndi chomwe chachititsa izo. Mwaona? Mipingo ili kuyesera kuti ikhale mwasayansi.

¹⁵⁴ Ndipo kumbukirani, pamene munthu akupindula chitukuko mwa sayansi, iye akudzipha yekha tsiku lililonse. Pamene iye anayambitsa wonga wa mfuti, taonani zomwe iwo wachita. Pamene iye anayambitsa galimoto, iyo imapha mochuluka kuposa momwe wonga wa mfuti umachitira. Tsopano iye wadzipezera yekha bomba la haidrojeni. Ndikudabwa chomwe iye ati achite nalo ilo? Kulondola.

¹⁵⁵ Ndipo chotero mmomwe uliri mpingo, pamene iwo ukuyesera kuti uzipindula mwa sayansi, mwa njira zopangidwa ndi anthu, izo zikukutengerani inu kutali kwambiri ndi Mulungu, ndi mu imfa, kuposa momwe izo zinaliri pa malo oyambirira. Ndiko kulondola. Musati muusankhe mpingo wanu mwa njira yofanana ndi momwe munachitira akazi anu. Mwaona? Chimene sayansi inamuchitira iye chinali chozizwitsa, koma inu ndibwino kuti mutalikirane kwa mpingo uli pa izo; iye anapanga utoto, wonga, ndi zinthu zina zonse izi. Muzisankha mwa khalidwe la Mawu Ake.

¹⁵⁶ Tsopano tiyeni ife tifanizire mkwatibwi wachibadwa wa lero ndi otchedwa mpingo wa mkwatibwi wa lero. Fanizitsani mkazi, akupita kuti akakwatiwe lero.

¹⁵⁷ Tsopano, tangoyang'anani chomwe sayansi yamuchitira iye. Iye amatulukira apo, poyamba, ali ndi tsitsi lake litadulidwamo, ali ndi kamodzi ka kakonzedwe ka tsitsi ka Jacqueline Kennedy aka, onani, kapena chinachake chonga izo. Ndipo inu mukudziwa zomwe Baibulo linanena? Baibulo makamaka limamupatsa mwamuna, ngati iye akufuna kutero, ufulu womusiya iye mu chilekano, ngati iye achita izo. "Iye ndi mkazi wosalemekezeka, yemwe angadule tsitsi lake." Baibulo linanena chomwecho. Kulondola. Simumadziwa izo? Nha? O, eya! Ine ndalalikira mochuluka kwambiri mu California kuti inu musazidziwe izo. Uko nkulondola. O, eya! Ndi ubwino wanji womwe izo zimandichitira ine? Iwo amachita izo, mulimonsebe. Inu simungakhoze kuitenga nkumba ndi kuisintha dzina lake, nkumupanga iye kukhala mwanawankhosa. Zindikirani.

¹⁵⁸ Inu mudana nane ine ndikatsiriza izi, koma inu muzidziwa Choonadi. Mwaona?

¹⁵⁹ Taonani. Tiyeni tifanizitse izo. Apa iye akubwera ali ndi kuchuluka konse kwa utoto, chinachake chomwe iye sali, mkwatibwi wamakono. Atamusukusulitsa nkhope yake, mwamunayo akanathawa kwa iye, mwinamwake. Angakuwopyeni inu pafupi kufa, atachotsapo zinthu zonse izo pa iye. Ndi momwe ziriri ndi mpingo uli ndi kutsogolo, kwakukulu kopentedwa, Max Factor wa fioroje yathunthu. U-nhu. Onsewo ali—ndi nkhope yokongola, yabodza pa iwo, kukongola kopangidwa ndi anthu ndipo osati kukongola

kopangidwa ndi Mulungu. Mulibe khalidwe lochuluka mwa aliyense wa iwo.

¹⁶⁰ Zindikirani, basi monga Satana, zokwanira kuti anyenge nazo, fanizirani mkwatibwi wamakono tsopano ndi iye: amavala akabudula, amavala utoto, amadula nalichotsa tsitsi lake, amavala zovala zomwe zimawoneka ngati za amuna, ndipo amamvera kwa m'busa yemwe anamuuzza iye kuti izo zonse zinali bwino. Iye ndi wonyenga. Iye adzakazunzika chifukwa cha izo mu madera a kutsidyalo. Uko nkulondola. Akuchita izo kuti azinyenga, kuti akhale chinachake chomwe iye sali.

¹⁶¹ Umo ndi momwe mpingo umachitira, umatenga DD. yaikulu, Ph.D., LL.D. Chotero kuti inu muziti, “Abusa athu ali ndi *ichi, icho*, ndi *chinacho*,” mwinamwake asakudziwa nkomwe za Mulungu kuposa Nkafula amadziwira za walupanga wachi Igupto. Uko nkulondola. Kulondola. Chokuchitikira china cha fioroje ya ku seminare kunjja uko, ndipo asakudziwa kalikonse za Mulungu kuposa chirichonse.

¹⁶² Mpingo wamakono ndi utoto wawo wafioroje, uli ndi akazi awo onse ulemere wawo utametedwa nuchotsedwa, ndi ricky wawo wina ndi m'busa yemwe iwo ali naye, monga Yezebeli ngati panayamba pakhala mmodzi. Tsitsi lodulidwa, akabudula, utoto, zonse zitakonzedwa monga mwa kufuna kwa fioroje, umo ndi momwe mpingo ukuimira. Kulondola. Koma khalidwe lake lauzimu liri kutali ndi kukhala womanga banja yemwe Yesu Khristu akubwera kuti adzambulandire.

¹⁶³ Ngati Mkhristu aliyense akanakwatira mkazi wonga uyo, izo zikusonyeza kuti iye wagwa kuchokera ku chisomo. Kafunidwe kake ka Mulungu ndi kafunidwe kake ka banja, lingakhale banja lotani, ziri kutali, pamene iye asankha mkazi wonga uyo. Ayi, bwana. Iye zedi sangakhoze kukwanira pa kafunidwe ka Chikhristu. Khalidwe lake lauzimu liri pa malo otsikitsitsa, lakufa, mu kukongola kwa chipembedzo ndi kusilira kwa dziko.

¹⁶⁴ Apo ndi ndendende pamene mpingo waima lero, wagulitsa khalidwe lake lopatsidwa ndi Mawu nupita kwa Satana, pofuna chipembedzo chasayansi chopangidwa ndi anthu. Pamene, iye anali nawo ufulu, monga mpingo wa Mulungu, kuti azikhalabe ndi Mawu a Mulungu ndi kumakhala nawo Mzimu Woyera ukugwira ntchito pakati pawo, akuliwocherera Thupilo palimodzi ndi Mawu ndi chikondi cha Mulungu. Mmalo mwa izo, iye anagulitsa maufulu obadwa nao ake, monga Esau, ndipo anatenga chipembedzo kuti chizimuloleza iye kumachita chirichonse chimene iye amachifuna kuchita, kulondola, kungoti akhale wotchuka monga amayi ake anachitira ku Nicaea Roma. Mawu a Mulungu!

¹⁶⁵ O, momwe izo zalowerera mu dera lathu la Chipentekoste! Ndi zoipa kwambiri, koma iwo unachita izo.

166 Zindikirani, miniti yokha, nani mu mpingo wa Katolika. Mkazi uyo, kuti akhale nani, ndi kutenga chophimba chotsiriza icho, iye ali wodzigulitsa mwamtheradi kwa mpingo umenewo. Iye ali (solo, thupi, ndi mzimu) chuma cha mpingo umenewo. Iye alibe malingaliro ake ake. Iye sangakhoze kukhala nawo, pamene iye atenga chophimba chotsiriza icho, wopanda lingaliro la iye mwini, wopanda chifuniro cha iye mwini. Onani kunja kuno, chomwe Satana akuwapangira iwo zonyengezera zake, ngati zoon.

167 Mpingo woona wa Khristu, Mkwatibwi, wadzigulitsa wokha kwa Iye ndi Mawu Ake olonjezedwa, mpaka malingaliro omwe amene ali mwa Khristu ali mwa inu. Kusiyana kwake!

168 Ndipo ife tikupeza lero, kuti, mpingo wamakono, mpingo wamakono wa mdziko. Mpingo wamakono wa mdziko ndiponso kuti mpingo wauzimu yonse ili ndi pakati, kuti ibale ana aamuna.

169 Mmodzi wa iwo, kubala kwachipembedzo, kudzachitika, tsiku lina, mu masiku awa, ku Bungwe la Mipingo ya Mdziko, yomwe iti idzepereke kwa dziko wotsutsakhristu, kupyolera mu chipembedzo. Ndizo ndendende Choonadi. Ine mwina sindikhala moyo kuti ndidzaziwone izo. Ine ndikukhulupirira kuti ndidzatero. Koma, inu anthu achichepere, muzikumbukira kuti inu munamumva mtumiki akunena izo. Zomwe ziti zidzatsiritse. Ndipo icho ndicho chilemba cha chirombo, pamene iye akupanga Bungwe la Mipingo ya Mdziko. Ndipo iye adzabala mwana wake, wotsutsakhristu.

170 Winawo uli ndi pakati pa Mawu a Mulungu ndipo udzabala Thupi, Thupi lotsirizidwa la Yesu Khristu, lomwe liri Mkwatibwi. Thupi la Khristu silinatsirizidwe panobe. Ndi angati akudziwa izo? Mwamuna ndi mkazi ali mmodzi. Ndipo Khristu ali Thupi limodzi, Mawu. Mkwatibwi ayenera kuti akhale Thupi lina lonselo. Ndipo awiriwo, palimodzi, akupanga Thupi limodzi kachiwiri. Monga Adamu analiri pa chiyambi: mwamuna, mkazi wake, ali mmodzi. Tsopano, Iye, Mkwatibwi woona, wodzigulitsa kwambiri kwa Iye, moti Iye samagwiritsa malingaliro Ake ake. Malingaliro ake, ndithudi, ali chifuniro Chake, ndipo chifuniro Chake ndicho Mawu Ake.

171 Tsopano tayang'anani pa wotchedwa-mkwatibwiyo wosankhidwa ndi mwamuna, ndipo mufanizitse wauzimu kwa wachibadwa wa lero, Yezebeli wamakona wolodzedwa ndi Ahabu wake, kukongola kwa Max Factor, chirichonse. Tayang'anani pa mpingo, njira yomweyo, koma wachiwerewere kwa Mawu a Mulungu wamoyo; zipembedzo zazikulu, nyumba zazikulu, ndalama zazikulu, malipiro aakulu, odzigulitsa yense. Amuna kumaima mu guwa nkumavomereza kuti izo zonse ziri bwino, ndi kumawaloleza iwo azipitirira nazo. Ndi chinyengo basi, ndizo zonse. Moonadi M'badwo wa

Mpingo wakhungu wa Laodikaya, ndendende basi chimene Baibulo linati ukanadzakhala uli. “Anati, ‘Ndine wolemera. Ine ndikukhala monga mfumukazi. Ine sindikusowa kanthu.’ Ndipo iwe sukudziwa kuti ndiwe wosauka, womvetsa chisoni, wakhungu, watsoka, wamaliseche: ndipo sukudziwa izo.” Ngati izo siziri PAKUTI ATERO AMBUYE, Chivumbulutso 3, ine sindinayambe ndawawerengapo Iwo. Ndi chimene iye ali, ndipo sakudziwa izo! Taganizani za izo.

¹⁷² Ngati inu mutamuuza mwamuna kapena mkazi, pa msewu, yemwe anali mbulanda, ndi kuwauza iwo kuti ali buno bwamuswe, ndipo iwo nkuti, “Zisamala ntchito yako yako,” bwanji, pali matenda aubongo apo penapake. Pali chinachake chomwe chalakwika ndi malingaliro awo.

¹⁷³ Ndipo pamene inu mungakhoze kuwerenga Mawu a Mulungu, momwe anthu ayenera kuti azichitira, ndi ubatizo uwu wa Mzimu Woyera umene ife tiri nawo lero, ndi, anthu, bwanji, iwo amayang’ana pa iwe ngati kuti iwe unali wamisala. Iwe ukawauza iwo, “Iwe uli. . . Iwo ayenera kuti abadwe kachiwiri. Iwo ayenera kuti azikhulupirira Baibulo.”

¹⁷⁴ Iwo amati, “Izo zinali nthano za Chiyuda, za zaka zapitazo. Mpingo wathu uli nayo njira.” Atsoka, omvetsachisoni, akhungu, amaliseche, ndipo sakudziwa nkomwe izo. Chomwe. . . Ndipo Baibulo linanena kuti icho ndi chikhalidwe chomwe iwo akulowamo.

Angakhoze bwanji mneneri woona kuphonya kuziwona izo? Ine sindikudziwa.

¹⁷⁵ Zikulowerera kumene mu mipingo yathu yonse, kulikonse. Tangoyang’anani pa izo, basi mwa kachitidwe kamakono. “Hule wakaleyo ndi anake aakazi,” wa Chivumbulutso 17, akupereka kwa anthu “osauka, akhungu, omvetsachisoni” chiphunzitso chake cha fioroje chosiyana ndi Mawu a Mulungu. “Ndipo iwo anapeza mwa iye miyoyo ya akapolo, ndipo amuna ndi akazi a— a kulikonse.” Mmallo mwa kuwakopa anthu. . .

¹⁷⁶ Khristu amawatsimikizira Mawu Ake, zomwe zimawakopa anthu. Iye samawakopera anthu ku mipingo yomwe imakopedwa ndi zipembedzo zazikulu ndi zochitika zazikulu, ndi zazikulu kwambiri zopitiriza ndi zinthu zamawonekedwe okopa. Koma Mawu a Mulungu amamukopa Mkwatibwi wa Khristu.

¹⁷⁷ Tsopano zindikirani. Ndi zosangalatsa k—kuzindikira momwe ziri kuti—kuti mpingo ukuyesera kuti uzikopa chidwi cha anthu ndi mikanjo yabwino ndi kwayala ovekedwa, ndi akazi odula tsitsi ndi nkhope zopentedwa. Ndipo iwo amaganiza. . . Ndipo iwo amaimba ngati Mngelo. Kunama ngati mdierekezi, kuthamanga thamanga usiku wonse kokavina, mosaganiza kanthu pa izo. Ndipo ndi zomwe iwo amaganiza, “Zonse ziri bwino. Izo ndi zokongola.” Koma, inu mukuona, izo ndi zopangidwa mwabodza. Awo si Mawu a Mulungu.

178 Pamene, Mkwatibwi woona amakopa chidwi cha Mulungu, powasunga Mawu Ake. Tsopano zindikirani. Tsopano tiyeni ife timuzindikire Khristu.

179 Inu mukuti, “Chabwino, tsopano, dikirani miniti, nanga bwanji kukongola uku kumene inu mukukukamba?”

180 Baibulo linati, mu Yesaya 53:2, kuti, pamene Yesu anabwera, “Panalibe kukongola kwa Iye, kuti ife tikhoze kumukhumba Iye.” Uko nkulondola? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Alibe kukongola. Ngati Iye akanati abwere mwa kukongola kwa chidziko, monga Satana aliri lero, anthu akanathamanga momuzungulira Iye ndi kumuvomereza Iye momwe iwo akuchitira nao mpingo lero. Iwo akanati amukhulupirire Iye, akanamulandira Iye, monga iwo akuchitira naye Satana lero. Ndithudi, iwo akanatero. Koma Iye sanabwere mu kukongola kwa mtundu umenewo, koma Iye nthawizonse amabwera mu kukongola kwa khalidwe. Apo, Khristu sanali Munthu wokongola, wamkulu, wamphamvu, wojintcha. Mulungu samausankha mtundu umenewo.

181 Ine ndikukumbukira nthawi ina mneneri anapita ku—kuti akamutenge mfumu, kuti akapange mfumu wochokera mwa wana a Jesse, kuti atenge malo a mfumu ina, Sauli. Ndipo chotero Jesse anamubweretsera iye, mnyamata wake wamkulu, wamphamvu, mnyamata wabwino. Iye anati, “Chipewa chiziwoneka bwino, pa mutu wake.”

182 Mneneri anapita kuti akatsanulire mafuta pa iye. Iye anati, “Mulungu wamukana iye.” Ndipo Iye anamukana wina aliyense wa iwo, mpaka iye anabwera kwa wamng’ono, wakaleyo wa mapewa-okugwa, kamunthu kowoneka-mofiira. Ndipo iye anatsanulira mafuta pa iye, ndipo iye anati, “Mulungu wamusankha iye.” Mwaona? Ife timasankha mwa mawonekedwe. Mulungu amasankha mwa khalidwe.

183 Khalidwe, sipanakhale konse khalidwe longa la Yesu Khristu. Ilo limakhala moyo mwa inu ndipo limawonetsera Iye. Ife tikuziwona izo nzoona. Si kukongola kwa chidziko kwa Iye kumene kumamukopa Mkwatibwi Wake. Ndi khalidwe Lake, khalidwe la Mpingo, limene Yesu anali kulifuna; osati kumene kuli nyumba zazikulu, kumene kuli zipembedzo zazikulu, kumene kuli umembala wawukulu. Iye analonjeza kuti adzakomana nao kulikonse kumene awiri kapena atatu asonkhana palimodzi. Zoonadi. Apo ndi pamene wokhulupirira woona amakhazikitsa ziyembekezo zake, ndi pa Mawu a Mulungu awo pokhala akutsimikiziridwa mu Choonadi, chomwe ali. Kusankha mwa Mawu Ake, osati gulu lokonda za chidziko. Iwo amadana nazo izo.

184 Palibe zodabwitsa iye akusudzulidwa kwa Iye, chifukwa iye waphonya vumbulutso Lake, ndipo iye alibe ilo. Iye samasamala

za iye, momwe iye amachitira ndipo akuchita, ndi kuchuluka kwa zinthu za mdziko izi zomwe ali nazo.

¹⁸⁵ Iye akufunafuna khalidwe lake, khalidwe la Khristu. Tsopano, mphindi yokha tsopano. Ndi choncho. Iye amamusankha Mkwatibwi kuti azinyezimiritsa khalidwe Lake, pomwe mipingo yamakono ya leroyi ndithudi ikuphonya d—dongosolo Lake apa, mailosi milioni, chifukwa iwo akuchikana *Ichi* kuti ndi Choonadi. Kotero kodi izo zingakhoze kukhala motani? Tsopano, Iye akuyembekezera tsiku lomwe Mkwatibwi ati adzawumbidwe, Ahebri 13:8, basi ndendende monga Iwo anali, monga Iye analiri. Iwo uyenera kukhala mnofu Wake wofanana, mafupa ofanana, Mzimu ofanana, chirichonse chofanana, ndendende basi zitamangidwa kuchokera, ndipo awiri awo ndiye akhale mmodzi. Mpaka mpingo ukhale izo, iwo sali mmodzi. Khalidwe la Iye, Mawu, a m'badwo uno, ziyenera kuti ziwumbidwe. Iye ayenera kuti awumbidwe monga Iye aliri.

¹⁸⁶ Tsopano, potseka, ine ndikufuna ndinene chifukwa chomwe ine ndinanenera zinthu izi, ndipo—ine nditseka. Usiku wina, pafupi 3:00 koloko mmawa ine ndinadzutsidwa.

¹⁸⁷ Ine nditenga aliyense wa inu kuti ayankhe izi. Kodi ine ndinayamba ndakuuzanipo inu chirichonse mu Dzina la Ambuye kupatula chomwe chinali cholondola? Izo nthawi zonse zakhala ziri zolondola. [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Kotero ndithandizeni ine, Mulungu akudziwa kuti izo nzoona. Palibe mmodzi wina, kulikonse mu dziko, mwa zikwi za zinthu zomwe zanedwa, zomwe Iye anayamba waphonyapo mawu amodzi a izo. Nthawizonse zakhala zikufika pochitika mwangwiro.

¹⁸⁸ Ngakhale mpaka pamene ine ndinali ku Phoenix, tsiku lina, kapena pafupi chaka chapitacho izo zinali, ndipo ndinakuuzani inu za Uthenga umenewo wa—wa *Ndi Nthawi Yanji Ino, Mabwana?* Ndipo ndinakuuzani inu, “Angelo Asanu ndi awiri ndikanati ndikakomane nao kunjira uko,” ndipo kudzakhala kutsegula kwa Zisindikizo izi, ndi chiani. Ndipo apo—magazini ya Life inalemba nkhanu ya izo, Lawi lalikulu ili likupita mmwamba mu mlengalenga, mailosi sate mmwamba, mailosi twente-seveni chotambalala. Iwo anati sankakhoza kuzindikira chomwe iwo unali; sakudziwa panobe. Ndipo amuna akhala pomwe pano mu nyumba ino usikuuno, anali ataima apo pomwe ndi ine pamene izo zinkachitika, ndendende basi zomwe Iwo ananena. Iye anandiiza ine zinthu zomwe zinkati zichitike, ndipo zinachitika basi ndendende. Momwe chirichonse cha Zisindikizo izo zinatsegulidwira, ndipo anandiiza zinsinsi zomwe zinali zitabisidwa mmusimo podutsa mu mibadwo iyo ya okonzanso ndi zina zotero, mwangwiro basi.

¹⁸⁹ Momwe, nditaima paja pamwamba pa phiri, amuna, atatu kapena anai a iwo aima pomwe pano tsopano, inde, oopera amenewo. Ndikupita chokwera phiri, Mzimu Woyera unati,

“Tola mwala uwo.” Ife tinali tikusaka. Iye anati, “Uponyere iwo mmwamba, ndi kuti, ‘PAKUTI ATERO AMBUYE.’” Ine ndinatero. Pansi kuchokera apo panadza fanulo yaing’ono ya mphepo. Ine ndinati, “Mkati mwa maora twente-foro, inu muwona dzanja la Mulungu.” Amuna akhala pomwe pano alipo tsopano.

¹⁹⁰ Tsiku lotsatira, pafupi teni koloko, nditaima apo, ine ndinati, “Konzekani. Pitani pansi pa galimoto apo, wa kunkhondo.” Ine ndinati, “Chinachake chikukonzekera kuti chichitike.” Umo munali mu mlengalenga moyera, mmwamba momwe mwa chigwa chachikulu. Pansi unabwera Moto wa kamvuluvulu kuchokera Kumwamba, basi mwamphamvu momwe Iwo ukanakhoza kufuulira, unagunda makoma monga choncho. I—ine ndinali nditaima pansi pomwe pa Iwo. Ine ndinavula chipewa changa, ndinagwira mutu wanga. Iwo unabwera pafupi mapazi atatu kapena anai pamwamba pa ine, ndipo unadula chidzenje mpaka cha ku khoma ilo monga choncho, ndipo linaphulika. Ndipo unabwereranso mmwamba mu mlengalenga, unazunguliranso kachiwiri, ndi kubwera pansi, nthawi zitatu, mpaka unadula pamwamba pa thengo la mitengo, kwa mayadi thuu handiredi. Mukuwamva anyamata awo akuti, “Ameni”? Iwo anali uko pamene izo zinkachitika, mukuona, ndipo kunapanga kuphulitsa kutatu.

¹⁹¹ Pamene iwo anatulukapo pansi pa magalimoto ndi chirichonse, nabwereranso uko, anati, “Uwo ukanakuwomba iwe, sakanati akhalepo malo amafuta.”

¹⁹² Ine ndinati, “Uyo anali—Uyo anali Iye. Iye anali kuyankhula kwa ine.” Mulungu amayankhula ndi kamvuluvulu. Mwaona? Ndipo apo panali Lawi la Moto lomwelo limene inu mumaliwona pa chithunzi, litaima pamene.

Ndipo pamene Ilo linapita mmwamba, iwo anati, “Ndi chiani kodi?”

Ine ndinati, “Chiweruzo chikukantha Gombe Lakumadzulo.”

¹⁹³ Tsiku lachiwiri kuchokera apo, Alaska anali pafupi kumira. Mwaona? Icho chinakantha kamodzi, apo, kumenya koyamba.

¹⁹⁴ Pamene, iwe umayenera kuti uchite chinachake, kuti uphiphirsire icho. Monga mwamuna yemwe anaika mchere mu nsupa, ndipo anawuponyera iwo mmadzi, ndipo anati, “PAKUTI ATERO AMBUYE, pakhale pali madzi okoma.” Ndi penanso, Yesu anatunga madzi ndipo anawatsanulira iwo mu chikho, n—ndipo anapanga vinyo kuchokera mwa iwo.

¹⁹⁵ Iwe umayenera kuti ukhale ndi chinachake, choti chiphiphirsire. Ndi chimene chija chinali, pamene unapita mmwamba mu mlengalenga ndi kubwera pansi. Iwo unayambitsa kamvuluvulu wamng’ono uja. Mkati mwa maora

twente foro, Iwo unali utaligwedeza phiri lija mpaka unadula gomo pozungulira iwo.

¹⁹⁶ Abusa Bambo Blair akhala apa, ine ndikuyang'ana kumene pa iwo tsopano, anali kuntunda uko ndipo anakatola zidutswa zina za Iwo, ndi zina zotero. Pano pali Terry Sothmann, iwo, ndipo aima pano, ndi Billy Paul. Ndi abale, ena a ambiri ena awa omwe akhala muno, omwe anali uko komwe nawona izo zikuchitika pamene Iwo unkaling'amba ilo.

¹⁹⁷ Izo sizopeka ayi. Icho ndi choonadi. Izo sizinali mmbuyo mu masiku a Baibulo. Izo ndi tsopano. Mukuona? [Osonkhana ati, "Ameni."—Mkonzi.] Mulungu uyo yemwe amene nthawizonse wandiwonetsa ine zinthu izi, ndipo izo zimafika pochitika, ndhendende mpaka pa chilembo. Palibe pomwe izo zinalephera nthawi imodzi. Tsopano ine ndikubwekerera pa Iye.

¹⁹⁸ Masabata angapo apitawo, ine ndinali mu masomphenya. Ndipo ine ndinali nditaima p—pa malo okwera, ndipo ine ndinali woti ndiwone kuwonetseratu kwa Mpingo. Ndipo ine ndinazindikira, akubwera kuchokera kwanga... Ine ndinali nditaima mochuluka ngati mwa njira *iyi*, ndikuyang'ana cha Kumadzulo. Ndipo akubwera njira *iyi* linali gulu lokondeka la akazi, kuvala kwabwino kwenikweni, tsitsi lalitali litakonzedwera bwino kumbuyo, mikono, ndi masiketi ofika pansu mwaluso. Ndipo iwo onse anali mwa nyimbo yoguba, monga, "Patsogolo, asilikari Achikristu, kuguba ngati waku nkondo, ndi mtanda wa Yesu ukupitabe patsogolo." Ndipo pamene iwo anali kudutsa apo, ine ndinaima, ndipo panali Chinachake apo, Mzimu wina, anali Mulungu, ndipo anati, "Ndi uyo Mkwatibwi." Ndipo ine ndinayang'ana, ndipo mtima wanga unali wokondwa. Ndipo Iye anapita kuzungulira mbali *iyi*, ndipo anadutsa kuzungulira kumbuyo kwanga.

¹⁹⁹ Patapita kanthawi, pamene iye anabwereranso njira *iyi*, Ilo linati, "Tsopano mpingo wamakono ukubwera mu kuwonetseratu." Ndipo apa unabwera mpingo wa Chimwenye. Ine sindinayambe ndawonapo gulu lanyansi chotero.

²⁰⁰ Apa panadza mipingo ina, ya fuko losiyana. Iyo inkawoneka moyipa.

²⁰¹ Ndipo i—ine ndikunena izi chifukwa ndine wokakamizidwa kuti ndizinena choonadi, pamaso pa Mulungu. Ndipo pamene Iye anati, "Apa pakudza mpingo wa Chimereka tsopano, kuti uwonetsedweretu." Ngati ine ndinayamba ndawonapo gulu la adierekezi, linali limenelo. Akazi amenewo anali atavula maliseche, ndi kanthu kena kowoneka-kotuwa, ngati mtundu wa chikopa cha njovu. Ndipo iwo anali akuchigwirizira icho kutsogolo kwao, kalibe gawo la kumtunda mwa iko konse. Ndipo iwo anali akuchita mtundu uwu wa zinthu, zomwe, z—zovina izi zomwe ana awa amapanga kunja kuno, omwe amadzipotokola ndi zinthu, ndi nyimbo za mtundu uwo

zikupitirira. Ndipo pamene ine ndinamuwona Abiti U.S.A. akutulukira, ine ndinatsala pang'ono kukomoka.

²⁰² Tsopano, izi ndi PAKUTI ATERO AMBUYE. Inu mukundikhulupirira ine kuti ndine wantchito Wake. Inu mundikhulupirire ine tsopano. Ine sindikanati ndinene izo pofuna kanthu kena mu dziko. Mulibe ndalama zokwanira mu dziko lonse zomwe zingandipangitse ine kuti ndinene izo ngati izo sizinali zoon.

²⁰³ Ndipo pamene iye anabwera cha apo, icho chinali chinthu chowoneka monyansa kwambiri chimene ine ndinayamba ndachiwonapo. Ine ndinaganiza, “Mulungu, molimba momwe alaliki ndi ife abale tavutikira kuti tikupezereni Inu Mkwatibwi, ndipo icho ndi chopambana chimene ife tikanakhoza kuchichita.” Iye anali akudzipotokola, akugwirizira *ichi* kutsogolo kwa iye, monga imodzi ya masiketi chinthu cha hula, atachigwirizira icho kutsogolo kwa ziwalo zake, gawo lake lammusi, monga *chonchi*, akuvina ndi kumadzipotokola monga ana awa amachitira kunja kuno pa... pa ziwonetsero zoipa izi zomwe iwo ali nazo, akudzipotokola. Ameneyo anali Abiti Chikhristu chamu Amereka.

²⁰⁴ Chotero ndithandizeni ine, mwa thandizo la Mulungu, ndi momwe izo zimawonekera pamaso Pake. I—ine basi...ine ndinayamba...Ine ndikanakhoza kukomoka. Ine ndinaganiza, “Kuyesera konse, ndi kulalikirira, ndi kukakamiza?” Wina aliyense wa iwo ali ndi tsitsi lodula, ndipo iwo anali akudzipotokola ndi kumapitiriza, akugwirizira *ichi* patsogolo. Iwo anabwera mozungulira, pamene ine ndinali nditaima apo ndi Chinthu chauzimu ichi. Ine sindinkakhoza kumuwonona Iye. Ine ndinkamumva Iye akuyankhula kwa ine; anali kumene pondizungulira ine. Koma pamene iwo anatembenukira njira *iyi*, iwo ankagwirizira *ichi*. Ndipo basi akudzipotokola ndi kumaseka ndi kupitiriza, kumapitirira monga choncho, akugwirizira *ichi* patsogolo pawo.

²⁰⁵ Tsopano, ine nditaima mu Kukhalapo Kwake apo, ndipo wantchito Wake. “Ndi zonse zomwe ine ndayesera, icho ndi chopambana chomwe ine ndikanakhoza kuchichita?” Ine ndinaganiza, “Mulungu, kodi izo zinandichitira ubwino wanji ine? Kodi izo zinachita ubwino wotani? Kulira konse, ndi kupempha, ndi kukakamiza, ndi zizindikiro zazikulu ndi zodabwitsa ndi zozizwitsa zomwe Inu mumasonyeza. Ndi momwe ine ndinkaimirira apo, ndi kupita kunyumba ndi kukalira nditatsiriza kulalikirira kwa iwo ndi zinthu, ndipo ndi ubwino wanji womwe izo zinandichitira ine? Ndiyeno ine ndidzayenera kuti ndidzapereke chinachake chonga izo kwa Inu, monga Mkwatibwi.”

²⁰⁶ Ndipo pamene ine ndinaima apo, ndikuyang'ana, iye anadutsa napitirira apo. Ndipo inu mukhoza kulingalira

gawo la kumbuyo kwa iye, wopanda chirichonse atachivala, anagwirizira *ichi* kutsogolo kwa iye pamene iye ankapita psyatapsyata nazo, monga choncho, mwakudzipotokola uku, akuponyera miyendo yake kunja monga choncho. Ndipo, iye, o, izo zinali zoipa, momwe iye anali akupitirira, thupi lake likugwedzedwa mozungulira monga choncho. Tsopano ine . . .

207 Inu mukuti, “Kodi izo zikutanthauza chiani, M’bale Branham?” Ine sindikudziwa. Ine ndikungokuuzani inu zomwe ine ndinaziwona.

208 Ndipo pamene iye anadutsa apo monga choncho, ine ndinayang’ana pa iye. O, ine ndinangofika pokomoka kwenikweni. Ine ndinangotenbenukira kwina. Ine ndinaganiza, “Mulungu, ine ndatsutsika. Pali—palibe chifukwa choti ine ndiziyesera kenanso. Ine basi ndikhoza kungosiya.”

209 Akazi a Carl Williams, ngati inu mwakhala pano, ndipo loto lija limene inu munandiuza ine, kanthawi kapitako, lomwe inu munali nalo usiku wina, lomwe lakhala likukuvutitsani inu. Ndi izo apo. Chiwongolero chachotsedwa kuchokera mu dzanja langa.

210 Ndiye, ine ndinangoganiza, “i—ine ndikhoza basi kungoziiwala izo. Ine ndinali nditapita.”

211 Ndiye, zonse mwakamodzi, ine ndinazimva Izo zikubwera kachiwiri. Ndipo atabwera apo kumbali *iyi* anabwera Mkwatibwi yemweyo yemwe anapita mozungulira kumbali *iyi*. Apa panabwera madona aang’ono aja kachiwiri, ndipo aliyense wa iwo anali atavala mu zovala za fuko lawo kumene iwo amachokerako, monga Switzerland, Germany, ndi kwina kotero, aliyense atavala mtundu wa chovala icho, onse atsitsi lalitali, ndendende basi monga ujayu wa poyamba. Ndipo apa iwo anali akubwera, akuyenda. “Patsogolo, asilikari Achikhristu, kuguba ngati waku nkondo.” Ndipo pamene iwo ankadutsa cha pamalo a kuwonetseratu pamene ife tinali titaima, basi zonse mwakamodzi, diso lirilonse linapita mbali imeneyo. Ndiyeno iwo anatembenukira mmbuyo, ndipo mopitirira iwo anapita, akuguba, ndipo basi pamene iwo anayamba kupita chokwera mu mlengalenga momwe.

212 Wina ujayu anapita ku mphepete ya phiri ndipo anapita mmusi, monga *choncho*.

213 Awa anayamba kuguba chokwera kupita mu mlengalenga momwe. Ndipo pamene iwo ankapita akuguba, ine ndinazindikira asungwana angapo aang’ono mmbuyomo, ankawawoneka ngati iwo akanakhala ali msungwana wina wakunja, monga Sweden kapena Switzerland, kapena kwinakwake. Iwo anayamba kuyang’ana pozungulira, ndipo anafika . . . Ine ndinati, “Musati muchite izo! Musati muchoke pa mayendedwe!” Ndipo pamene ine ndinafuula monga choncho, ine ndinagalamura, mu masomphenya, nditaima apo ndi

dzanja langa lotambasula monga *choncho*. Ine ndinaganiza, “Chabwino...”

214 Nchifukwa chake ine ndanena zomwe ine ndinanena, usikuuno. Ine ndikufuna kuti ndikufunensi inu funso. Kodi ndi mochedwa kuposa momwe ife tikuganizira? Kodi Iye angakhoze kukhala kuti waitanidwa kale ndi kusankhidwa, wasindikizidwa azipita? Sipakhala mmodzi wina wowonjezera, inu mukudziwa. Kodi izo zingakhoze kukhala zotheka? O, eya. O, eya.

215 Kumbukirani zomwe ine ndinanena, tsiku lina pa kadzutsa. Mu umuna wa kubalitsa yamphongo ndi yaikazi, pamakhala mamilioni a nyongolosi zomwe zimapita umo, mazira milioni amapita apo. Koma pamakhala limodzi lokha la iwo limakhala moyo, ndipo apobe, iliyonse ya izo zofanana basi: Mmodzi pa milioni. Aliyense ya izo, dzira lofanana ndi mtundu wofanana wa nyongolosi. Mmodzi wa iwo amakhala moyo. Ena onsewo amafa.

216 Palibe wina yemwe angadziwe kuti ndi liti lomwe liri dzira lakucha, ndi, o, chiani cha izo. Mulungu amayenera kulingalira pa izo, kaya akhala mnyamata kapena msungwana, tsitsi lofiira kapena labulauni, kapena chirichonse chomwe ati adzakhale ali. Mulungu amalingalira pa izo. Osati zoyamba kukomanazo, koma zoyamba zomwe Mulungu azilingalira. Mwina mmodzi kubwera pamwamba *apa*, ndi limodzi. . . Ngati inu munayamba mwazindikirapo, mu chubu choyesera, kuti muziwone izo zikubwera pamodzi. Ine ndinaziwonapo izo. Mulungu amayenera kuti alingalire izo. Mmodzi, aliyense wa iwo, ofanana basi, koma mwa kusankha. Kubadwa kwachilengedwe ndi mwa kusankha. Mulungu amamutenga mmodzi kuchokera pa milioni.

217 Pamene Israeli anachoka ku Igupto, pa ulendo wawo waku dziko lolonjezedwa, iwo anali pafupifupi anthu mamilioni awiri. Aliyense wa iwo anali pansi pa mwanawankhosa wansembe yemweyo, kapena iwo sakanati akhale moyo. Aliyense wa iwo ankamvetsera kwa Mose, mneneri. Aliyense wa iwo anabatizidwira kwa iye, mu Nyanja Yofiira. Aliyense wa iwo anavina, akazi limodzi ndi Miriamu, chokwera-ndi-kutsika mu mbali ya (pamene) gombe la nyanja, pamene Mulungu anamuwongera mdaniyo. Aliyense wa iwo anaima ndi Mose, ndipo anamumva iye akuimba mu Mzimu. Iwo, aliyense, anadya manna ochokera mchipululu, omwe ankagwa pansi kuchokera Kumwamba. Manna atsopano, usiku uliwonse, chomwe chiri choimira cha Uthenga, aliyense wa iwo anadya pa iwo. Koma, kuchokera mu mamilioni awiri, ndi angati anakafikako? Awiri. Mmodzi kuchokera pa milioni.

218 Alipo pafupifupi Akhristu mamilioni mazana asanu mdziko usikuuno, kuwerengetsa Akatolika ndi onse. Mamilioni mazana asanu otchedwa okhulupirira mdziko. Ngati Mkwatululo ungadze usikuuno, izo zingatanthauze. . . ngati ali mmodzi pa milioni

kukanakhala kuwengerako. Ine sindikunena kuti iko kuli. Koma ngati uko kukanakhala, anthu faifi handiredi, mu maora twente-foro otsatirawa, akanati akhale atasowa. Inu simukanakhoza ngakhale kumva za izo. Adzakhalapo ochuluka chomwecho akusowa, mulimonse, sangakhoze ngakhale kuwengeredwa.

²¹⁹ Ndiye izo zikhoza kukhala, kutichitikira ife, amzanga, monga izo zinachitikira pamene Yohane M’batizi anadza. Ngakhale ophunzira anati, “Chifukwa chiani Malemba amati, chifukwa chiani—atumwi kapena aneneri amati? Nchifukwa chiani zimanenedwa kuti Eliya ayenera kubwera poyamba ndi kudzabwezeretsa zinthu zonse?”

²²⁰ Iye anati, “Ine ndikunena kwa inu kuti Eliya wabwera kale, ndipo inu simunazidziwe izo.”

²²¹ Limodzi la masiku awa ife tidzakhoza kusiyidwa titakhala pano, “Nanga bwanji za Mkwatulo chisautso chisanayambike?”

“Izo zabwera kale ndipo inu simunazidziwe izo.”

²²² Thupi lonse, litasindikizidwira mkati, kumangowusunga Iwo mu mayendedwe. Ine sindikunena kuti izo ziri mwanjira imeneyo. Ine ndikuyembekeza kuti izo siziri mwanjira imeneyo. Koma, mzanga, pamene izo tiyeni . . .

²²³ Ngati ife tiri nako kumverera mu mtima mwathu, usikuuno, kuti ife tiyenera kukonza miyoyo yathu, ndi zinthu zomwe ife tazichita, ndiloleni ine ndikulangizeni inu, monga m’bale wotumikira. Ine ndikuti ndinene izi kwa nthawi yanga yoyamba, pa guwa. Ine ndatambasula motalikira usikuuno, pa *Izi*, kuposa momwe ine ndachitirapo pa china chirichonse, nthawi iliyonse, mulimonse, pamaso pa gulu, chifukwa ine ndakhala nawo ufulu waukulu mu misonkhano iyi. Ngati inu mukundikhulupirira ine kuti ndine mneneri wa Mulungu, inu mumvetsere ku zomwe ine ndimakuuzani inu. Ngati pali kachidutswa kakang’ono ka kumverera mu mtima mwanu, inu mupite kwa Mulungu pakali pano. Inu muchite izo.

²²⁴ Imani miniti yokha, amuna. Tayang’anani pa tanu—tizikhulupiriro tanu tomwe inu mumatitumikira. Tayang’anani mu mipingo yanu. Kodi izo ziri ndendende basi ndi Mawu a Mulungu? Kodi inu mwakwaniritsa choyenera chirichonse? Mukuti, “Ndine munthu wabwino.” Mmomwe analiri Nikodimo, ndi momwenso analiri onse a iwo. I—iwo anali abwino. Mwaona? Izo zilibe kanthu kochita ndi Iwo.

²²⁵ Ndipo, akazi, ine ndikufuna kuti inu muyang’ane mu kalilole, ndi kuyang’ana chimene Mulungu akuchifuna kuti mkazi azichita. Ndi kuwona mu kalilole wa Mulungu, osati mu kalilole wa mpingo wanu tsopano, mu kalilole wa Mulungu, ndipo muwone ngati inu mungayeneredwe kukhala, mu moyo wanu, Mkwatibwi wauzimu wa Yesu Khristu.

226 Atumiki, ganizani mofanana. Kodi inu mukudula ngodya apo, kuti mupulumutse kumverera kwa winawake kutali uko? Kodi inu mukanachita *ichi* ngati izo zikanati zisakhale... ndipo iwo akanati akutulutseni inu mu mpingo? Ngati inu mukumverera mwanjira imeneyo, m'bale wanga wokondedwa, ndiloleni ine ndikuchenjezeni inu, mu Dzina la Yesu Khristu, thawani kwa izo pakali pano.

227 Ndipo, dona, ngati inu simungakhoze kukwanira pa chiyeneretso cha Mkhristu, osati ngati Mkhristu mwadzina, koma mu mtima mwanu, ndi moyo wanu zikufanana ndendende monga chikalata chaukwati cha Mulungu apa chikuti izo zimayenera kukhala ziri.

228 Ndipo, membala wa mpingo, ngati mpingo wako suli monga chomwecho, wosakhoza kukwanira pa chiyeneretso cha Mulungu cha Mawu Ake, chokani kwa izo ndi kukalowa mwa Khristu.

229 Ilo ndi chenjezo lotsimikiza. Ife sitikudziwa nthawi yake, ndipo inu simukudziwa nthawi yake, yomwe mzinda uno tsiku lina udzakhala uli apa pansi pa nyanja iyi.

230 “O, Kaperna,” anatero Yesu, “iwe yemwe wadzikweza mpaka kumwamba, udzabweretsedwa pansi mu gehena. Pakuti, ngati ntchito zamphamvu zikanati zichitidwe mu Sodomu ndi Gomora, iye akanakhala akuima mpaka lero.” Ndipo Sodomu, Gomora ali pansi pa Nyanja Yakufa. Ndipo Kaperna ali pansi pa nyanja.

231 Iwe mzinda, yemwe umadzitcha kuti ndiwe mzinda wa Angelo, yemwe wadzikweza wekha mpaka kumwamba, ndi kumatumiza nyansi zonse, zinthu zoipa za mafashoni ndi zinthu, mpaka ngakhale maiko akunja amabwera kuno kudzatengera zauve zathu ndi kuzitumiza izo kwina, kwa mipingo yako yabwino ndi nsanja, ndi zina zotero, momwe iwe ukuchitira. Kumbukira, tsiku limodzi iwe udzakhala uli pansi pa nyanja, masa ako a uchi ali pansi pakopo pakali pano. Mkwiyu wa Mulungu ukukhavukira pansi pa iwe pomwepo. Ndi motalika bwanji momwe Iye ati achigwire chotchinga cha mchenga icho chitapachikika pamwamba pakepo? Pamene, nyanja iyo uko kutsidyako, kuya kwa mailo, idzakagwera mmenemo, mpaka ku Nyanja ya Salton. Zidzakhala zoipirapo kuposa tsiku lotsiriza la Pompeii. Lapa, Los Angeles.

232 Lapani, nonse inu, ndipo bwererani kwa Mulungu. Ora la mkwiyo Wake liri pa dziko lapansi. Thawani pamene ikadalipo nthawi yoti muthawe, ndi kubwera mwa Khristu.

Tiyeni ife tipemphere.

233 Wokondedwa Mulungu, pamene, mu mzimu wanga, mukugwedezeka, mtima wanga ukuwukha madontho a misozi ya chenjezo. Perekani, O Mulungu, kuti amuna ndi akazi asadzaganize zomwe ine ndanenazi ngati nthabwala, ndipo

anthu a mpingo asaganize za izo ngati chinachake chimene chinali chokondera kapena chowatsutsa iwo. Mulole iwo awone, Ambuye, ziri mwa chikondi.

²³⁴ Inu mundichitire ine umboni, Mulungu Wamphamvuzonse, kuti kukwera-ndi-kutsika mchigwa ichi ine ndayenda, chaka ndi chaka, kulengeza Mawu Anu. Ndichitireni ine umboni, O Mulungu, ngati izo zikanati zichitike usikuuno, ine ndanena Choonadi. Inu mukuwadziwa masomphenya awa a Mkwatibwi ali Choonadi. Ine ndatenga Dzina Lanu mwa iwo, Ambuye, ndipo ndati kuti izo zinali PAKUTI ATERO AMBUYE. Ndipo ine ndikumverera kuti ine ndikudziwa, Ambuye, zomwe ine ndikuchita.

²³⁵ Kotero ine ndikukupemphani Inu, Ambuye, mu Dzina la Yesu, muwalole anthu adzigwedeze okha, usikuuno, ndi kuthawa ku mkwiyo umene uli nkudza, pakuti Ikabodi yalembedwa pa zitseko ndi pa mafuko. Chizindikiro cha mandalasi akuda chabwera pa iwo. Mzimu wa Mulungu wakwiyitsidwa nuchoka kwa izo, ndipo iwo ayezedwa mu zoyezera ndipo apezeka operewera. Phwando la Mfumu Nebukadinezara labwereza kachiwiri, ndi maphwando oledzera ndi akazi ovala mwatheka, odzitcha okha Akhristu.

²³⁶ O Mulungu wa Kumwamba, chitirani chifundo pa dziko lochimwa ndi anthu ochimwa, Ambuye, momwe ife tiriri usikuuno. Mulungu, ine ndikuyesera kuima pakati ndi kupempha chifundo Chaumulungu, kuti Inu muyankhule kwa khamu ili usikuuno ndi kumuitanira Mkwatibwi Wanu ku tcheru, Ambuye, kuti agube osati mwa chizindikiro cha kachikhulupiriro kalikonse, koma mwa kuwomba kwa Uthenga wa Ambuye Yesu Khristu. Perekani izi, O Mulungu. Mulole izi zidziwike, usiku uno, kuti Inu ndinu Mulungu, ndipo Mawu Anu ali Choonadi. Pamene, motsimikiza, mu nkhope za anthu awa, ife tikuwaitanira iwo ku tcheru cha Mawu Anu.

²³⁷ Mu Dzina la Yesu Khristu, ine ndikuwapempherera iwo, Ambuye. Iwo akuwonani Inu, kupyola mthunzi wa kukaikira uliwonse, mukusuntha kudutsa pa yinyinji wawo ndi kuwauza iwo zomwe ziri mu mtima mwawo. Ndipo Inu mukudziwa, Ambuye, izo, pakali pano, zomwe zikuchitika. Inu mukudziwa kuti izo ndi Choonadi, O Mulungu. Ndipo ine ndikukupemphani Inu, mu Dzina la Yesu, mulole Mzimu Woyera uyimire pakati kachiwiri, Ambuye, ndi kukoka kuchokera mwa omvetsera awa, Ambuye, awo omwe analembedwa mu Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa. Perekani izi, O Mulungu. Ine ndikupemphera ndi mtima wanga wonse.

²³⁸ Anthu awa, mwachibadwa, Ambuye, iwo akhoza kundipatsa ine kobiri lotsiriza lomwe iwo ali nalo, kuti athandizire Uthengawu. Iwo angachite chirichonse chimene iwo angakhoze. Koma, O Mulungu, pamene izo zifika pogwirizana ndi Iwo,

ndi kubwera mwa Iwo, ine ndikupemphera, Mulungu, kuti uno ukhale usiku womwe Inu muti muwapatse iwo mphoto ndi kutsanulira pansi Mzimu Wanu Woyera pa msonkhano waukulu uno. Ndipo mulole pasadzakhale pali zachisangalalo kapena kulumpha lumpha, koma kulira ndi kufuula, ndi kulapa, kugwiritsa ku nyanga za guwa, pamene ife tikuwona ziweruzo zikubangula pansi pa ife, usikuuno. Perekani izi, Mulungu. Ine ndikupemphera modzipereka momwe ine ndikudziwira, mu Dzina la Yesu Khristu.

²³⁹ M'bale wanga, mlongo, i—ine sindikudziwa zinanso zoti ndinene, ngati ine ndingapeze chisomo pamaso panu, mwa mphanvu ya Mulungu, ngati inu mukundikhulupirira ine kuti ndine mneneri Wake. Ino ndi nthawi yoyamba pa gulu yomwe ine ndinanenapo konse izo. Koma ine ndikumverera kuchenjeza kwachirendo kwa mtundu wina. Ine sindine wozolowera izi. Inu mukudziwa ine sindiri. Ine sindimachita monga chonchi. Ine ndimadodoma kuti ndiuyankhule Uthenga umenewo ndi kunena zinthu zimenezu. Ine ndathamanga chammbali ndi china chirichonse, kuti ndipewe kuchita izo. Koma Izo zanedwa kale, ndipo Izo zidzaima pa Tsiku la Chiweruzo, ngati umboni kuti ine ndakuuzani Choonadi. Ndizo PAKUTI ATERO AMBUYE MULUNGU! . . . ? . . .

²⁴⁰ O, Pentekoste, thawitsani moyo wanu. Thamangirani ku nyanga za guwa ndi kukalira, zisanafike mochedwa kwambiri, pakuti ora lidzabwera pamene inu mudzakhoza kulira ndipo izo sizidzakuchitirani inu ubwino uliwonse. Pakuti Esau anafuna kuti apeze malo, a ufulu wobadwa nao wake, ndipo sanakhoze kuwapeza iwo. Ine ndikukupereka iwe, o, California. O, msonkhano wawukulu wa Amuna Amalonda a Uthenga Wathunthu, omwe ine ndimawakonda, omwe ine ndawasiya ndi kudzimangirirako, ndi mtima wanga wonse, ine ndikukuperekani inu kwa Yesu Khristu, usikuuno. Thawirani kwa Iye! Musati mulole Mdierekezi akuziziritseni konse inu kwa Ichi. Khalani kumene ndi Icho mpaka inu, aliyense, atadzazidwa ndi Mzimu Woyera, mochuluka chotero, kuti zikupangitseni inu kubwera ku Mawu awa, omwe ati akupangitseni inu akazi kuwongoka, omwe ati akupangitseni inu amuna kuwongoka. Ngati inu mukunena kuti muli nao Mzimu Woyera, ndipo suli kugwirizana ndi Mawu, uwo ndi mzimu winawake mwa inu. Mzimu wa Mulungu umakhala pa Mawu Ake, Waumesiya, Mawu odzozedwa. Mkwatibwi ayenera akhale ka-Mesiya, Mawu odzozedwa.

²⁴¹ Tiyeni ife tiimirire pa mapazi athu, mu Dzina la Ambuye Yesu Khristu. Ngati inu simudzamva konse mawu anga kachiwiri . . . Koma, Mulungu akalola, ine ndikuyambapo waku Afrika, mu maora pang'ono. Ine mwina sindikabwerera. Ine sindikudziwa. Koma ine ndikukuuzani inu, ndi mtima wanga wonse, ine ndakuuzani inu Choonadi. Ine sindinapewe

kufotokoza kwa inu chirichonse chimene Mulungu anandiuza ine kuti ndinene. Ndipo ine ndazinena Izo mu Dzina la Ambuye.

²⁴² Ndi mphindi yotsimikiza. Ine sindikudziwa momwe ndingafotokozere izo. Ine ndayesera kuti ndichoke paguwali nthawi zitatu kapena zinai, ndipo ine sindikukhoza kuchita izo. Lino ndi ora lotsimikiza. Musati mudzaiwale konse izi. Ino ndi nthawi yomwe, mwinamwake, Mulungu akhoza kukhala kuti akupanga kuitana kwake kotsiriza. Ine sindikudziwa. Iye adzapanga kuitana Kwake kotsiriza, tsiku lina. Liti? Ine sindikudziwa. Koma ine ndikukuuzani inu, molingana ndi masomphenya aja, izo zikuwoneka ngati kuti Mkwatibwi watsala pang'ono kutsirizidwa.

²⁴³ Tayang'anani pa mipingo mwadzina ikubweramo. Pamene namwali wopusa anabwera kudzafuna Mafuta, iye analephera kuwapeza Iwo. Mkwatibwi anakalowa mkati. Mkwatulo unapita mmwamba. "Pamene iwo anapita kukagula Mafuta, Mkwati anabwera."

²⁴⁴ Kodi inu mwagona? Dzukani, msanga, ndipo mubwere kwa inueni. Ndipo tiyeni ife tipemphere, aliyense, ngati kuti ife timafa miniti ino, mu Dzina la Ambuye. Tiyeni, aliyense, mupemphere mwa njira yanu yomwe.

²⁴⁵ Mulungu Wamphamvuzonse, chitirani chifundo pa ife. Ambuye, chitirani chifundo pa ine. Chitirani chifundo pa ife tonse. Zitichitira ubwino wanji ife, ziribe kanthu chimene ife tingachite, ngati ife tilephera mu zinthu izi? Ine ndaima ndipo ndikupempha chifundo, O Mulungu, mzinda wawukulu uwu usanamire pansu pa nyanja ndi ziweruzo za Mulungu zisanasese ku gombe ili. Ine ndikupemphera, Mulungu, kuti Inu mumuitane Mkwatibwi Wanu. Ine ndikuwapereka iwo kwa Inu tsopano, mu Dzina la Yesu Khristu. Amen.



KUSANKHA KWA MKWATIBWI CHA65-0429E
(The Choosing Of A Bride)

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham woperekedwa mu Chingerezi Lachinayi usiku, Epulo 29, 1965, ku Biltmore Hotel mu Los Angeles, California, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingerezi. Kumasulira uku kwa Chichewa kunadindidwa m'chaka cha 2006 ndi Voice of God Recordings:

CHICHEWA

©2006 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org